


IMVANI LIWU LAKE

 Zikomo inu, M'bale Neville. Ine ndikukhulupirira izo zinanenedwa ndi Davide, "Ine ndinakondwera pamene ananena kwa ine, tiyeni ife tipite ku nyumba ya Ambuye." Pali chinachake basi chokhudza Sande sukulu chimene magawo ena a utumiki alibe, nthawi ina iliyonse kudutsa mu tsiku. Ife tangodzuka kumene kuchokera ku mpumulo wa usiku wabwino, ndipo—ndipo ife timangomverera mosiyana, ndipo inu mwatsitsimutsidwa ndi kukonzekera tsikuli.

² Tsopano ife tikumvetsa izo... Usiku watha, ife tinafunsa a—anthuwo ngati iwo anali nawo mpingo wawo...umene iwo anali kupitako, pamene akuchezera kapena—kapena... Ine ndikutanthauza, mamembala okhazikika a mipingo, kuti iwo akakhale ku mpingo wawo womwe mmawa uno. Chifukwa, ife pokhala azipembedzo zosiyanasiyana, ife sitimakonda basi kuwatenga anthu kuchoka ku gulu lawo lomwe.

³ Ndipo ine ndimatsutsidwa nthawi zambiri za—za kutsutsa mipingo ina. Uko nkulakwitsa. Ine sindimatsutsa mipingo ina. Ine ndimatsutsa, nthawi zambiri, zinthu zimene—zimene iwo amavomereza, koma ine ndithudi sindimatsutsa mpingowo. Koma, nthawi zambiri, pamene iwo aphunzitsa zinthu zomwe ziri zosiyana ndi Malemba, ndiye ine—ine ndimazitsutsa izo. Ndiyeno pamene iwo achita zinthu zomwe ziri zauchimo, ndi—ndi kumazilola izo kuti zizichitidwa mmipingo yawo, ine ndimazitsutsa izo. Koma osati...Monga momwe zimanenedwera...Ine ndiri nawo abwenzi ambiri Achikatolika akhala pano, ndipo ine sindimawatsutsa konse anthu Achikatolika. Ine ndimatsutsa chiphunzitsa cha mpingo wa Katolika, chifukwa ine sindimakhulupirira kuti chiri Mwamalemba. Ndipo osati mochuluka kuposa momwe ine ndimatsutsira iwo kuposa momwe ine ndimachitira ambiri a zipembedzo za Chiprotestanti, chifukwa ine sindikuganiza kuti izo ziri Mwamalemba. Ndipo ine ndiri wokakamizika kuyimira chimene chiri Choonadi. Mukuwona? Inu mukudziwa, Mulungu adzakuyamikirani inu ngati inu mukhala woona mtima, odzipereka basi.

⁴ Inu mukudziwa, nthawi zambiri, mwamuna wofunafuna mkazi, mwamuna weniweni yemwe ali ndi mwamuna kumbuyo kwake, iye samafunafuna konse msungwana yemwe ali wokongola kwambiri mu nkhope, kapena zina zotero. Iye amadziwa kuti iko kudzatayika, limodzi la masiku awa. Mukuwona? Iye amayang'ana mkazi yemwe ali mkazi mu umunthu, mkazi weniweni. Ndipo ngati iye ali wokhulupirika, ndi mkazi weniweni, mwamuna ameneyo adzamuyamikira iye. Ine sindikusamala ndi mochuluka bwanji—munthu woipa

bwanji iye ali, ndi mochuluka momwe iye amathamangira ndi—ndi akazi oipa; kulibe mwamuna woyipa mu dziko lapansi koma amene angayamikire mkazi amene angayime pa chimene mkazi ayenera kukhala. Uko nkulondola. Chifukwa, iye amayamikira zimenezo.

⁵ Ndipo umo ndi momwe izo zimakhallira mwa—mwa kulalikirira Mawu, ngati munthu ati ayime ndi zomwe iye amakhulupirira. Tsopano osati... Inu mukukumbukira, Mulungu amadziwa mtima wanu. Ndipo ngati inu muyima nacho chimene inu mukukhulupirira kwenikweni kuti ndi Choonadi, ndiye inu mukhoza kukhala nacho chikhulupiriro mu chimene inu mukuchikamba.

⁶ Ine ndiri nawo abwenzi abwino kuno. M'bale Charlie Cox, ine ndikumuwona atakhala kunjira uko. Ndipo masabata angapo apitawa, ine ndakhala ndiri mu Kentucky ndi iye, kusaka agologolo, kumene ine ndimapeza mpumulo wina. M'bale Banks Wood. Ndipo, tsopano, ife, tikuphonzira mu mfuti zathu, iwo. . . Ine ndinangoyenera kukhala ndi yanga yangwiro kwambiri mwakuti iyo imawombera nsomali pa mayadi fifite, kapena ine—ine basi sindingathe kusaka. Mukuwona? Ndizo zonse.

⁷ Chabwino, ndi ubwino wanji kuwombera nsomali? Mukuwona? Chifukwa, ngati inu mukuwombera pa gologolo, ndipo kuwombera kumutu, ndipo mutu wake mwina ndi waukulu mozungulira *choncho*, paliponse mkati mwa gulu la inchi zikhala zabwino, mwawona, paliponse mmenemo. M'modzi aliyense wa anyamatawo amati, “Ndizo zabwino. Ine ndamumenya gologoloyo.” Iwo amapitirira ndi kukamutenga gologoloyo. Koma, kwa ine, izo ziyenera kukhala zangwiro basi. Iyo iyenera kugunda kansomaliko. Iyo singakhoze kuphonya kotala la inchi. Iyo iyenera kumenya m'mbali mwa nsomali, kapena ine ndimangokhala wamanjenje ndi kukhumudwa.

⁸ Ndipo ine ndinali nditakhala pansu, tsiku lina, mu nkhalango, ndipo ine ndinali kunena, “Ambuye, chifukwa—chifukwa chiyani ine ndiri chidempete chotere? Chifukwa chiyani Inu munandipanga ine kuti ndikhale chidempete chotere?” Ine ndinati, “Tsopano apo. . .”

⁹ M'bale Banks anapita kukasaka ndi mfuti yake, ndipo iye anayikokera iyo kuti ayiwombere iyo mkati, ndi zoyang'anira za telesikopu. Ndipo inu basi. . . Kamodzi pa nthawi, mumatero. . . mmodzi amaphonya, chifukwa ngati iyo. . . Zipolopolo zoikidwa ku fakitale zimachita izo, mulimonse, chifukwa inu mumakhala ndi wonga wochulukirapo pang'ono, ndi wonga wocheperako pang'ono. Koma izo zimangomenya pambali pang'ono pokha, kapena inchi kapena awiri, M'bale Banks amatero, “O, izo ziri bwino, ine ndamumenya gologoloyo. Izo zonse nzabwino.” Izo sizitero—izo sizimamuvutitsa iye. Charlie, mwanjira yomweyo. Koma ine. . .

¹⁰ Yanga imayenera kumenya kansomali, pakati pomwe, kapena izo zimandikhumudwitsa ine. Ine ndinati, “Ine ndakhala chidempete mwachizolowezi.” Ndipo kenako ine ndinayamba kuyang’ana mmbuyo, ndipo ine ndinapeza kuti moyo wanga uli monga choncho. Ndiwo mapangidwe anga. Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, chifukwa chiyani Inu munandipanga ine monga choncho?” Izo zimandipangitsa ine kukhala wamanjenje ngati—ngati icho chipita pambali pang’ono pokha mwanjira *iyoy* kapena njira *iyoy*. Ndipo umo ndi momwe ndiye Ambuye anaululira kwa ine, nditakhala panso pamenepo, pamwamba pa Glutton Hollow, kulikonse kumene ife tinali, tikusaka. Iyo, ine ndikukhulupirira iyo imatchedwa Dutton; koma, agologolo amadya mwachangu kwambiri, ine ndimatcha iyo, “Wosusuka.” Kotero iwo. . .

¹¹ Pamalo awa, ine ndinaganiza, “ndi zimenezo.” Ine sindikanaphunzitsa ngakhale kuti kuli gehena mpaka ine nditatsimikiza za izo. Mukuwona? Ndipo chotero ngati Lemba likuneneratu machiritso Auzimu, ndipo *apa*, zikuwoneka monga *chonchi* ndi monga *choncho*; ngati Lemba limati, “Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera,” monga pali Amulungu atatu, ndipo *Apo* ine ndimawona pali Mmodzi yekha; ndipo tsopano ine ndingachite bwanji mwachisawawa, za anthu ena, zomwe iwo amanena za Iwo, kuzitenga izo monga choncho? Ngati Baibulo limayankhula za kukonzedweratu ndi chisomo, ndipo *apa* izo ziri nazo ntchito, ndipo *apa* izo ziri nacho chisomo. Ndipo ine—ine sindingakhoze basi kuzilalikira izo monga choncho.

¹² Ine ndiyenera kuzithetsa izo, ndipo kudzera, ndi kudzera, ndi kudzera mu Baibulo, mpaka izo zikuwongolera mwangwiro kansomali, mwawona, mpaka izo zitatuluka mwangwiro kwenikweni kudzera M’malemba. Ndiye pamene ine ndiima, ine ndikhoza kwenikweni kukhala nacho chikhulupiriro mu chimene ine ndikuchita, mwawona, kudziwa kuti chimene inu mukulalikira ndi Choonadi. Mukuwona? Ndipo kenako ngati aliyense atsutsa za Izo, inu mwaphunzira kale mokwanira mpaka inu mutadziwa ndendende basi zomwe Iye akunena, pamene inu mungamuyimitse iye, mwawona, pompa *Apa*. Mukuwona? Ndipo umo ndi momwe izo ziliri. Mulungu amatipanga ife mwanjira zosiyana, kuti ife tingakhoze basi mophweka. . . Izo zimapangitsa dziko kukhala mwanjira imeneyo. Koma, ndizo zomwe zimandipangitsa ine kukhala wamanjenje chotero, mtundu wokhumudwitsidwa wa munthu. Izo ziyenera kukhala zolondola basi.

¹³ Ndipo ndine wokondwa kwambiri, usikuuno, lero, uno—mmawa uno, kuti ndinene kuti ine ndikudziwa kuti Ambuye Yesu sali wakufa. Iye ali wamoyo, ndipo Iye ali mochuluka pomwe pano tsopano monga Iye analiri nthawi iliyonse mdziko ku Galileya kapena kwina kulikonse. Iye ndi Mwana wamoyo,

wowukitsidwa, wopezeka paliponse wa Mulungu wamoyo. Ndizo. . . Ndipo ngati ine sindikanakhoza . . .

14 Ngati ine ndikanaphunzitsa Lemba la Mulungu wina wa mbiriyakale, ndipo ine sindinali wotsimikiza kuti Iye anali pomwe pano, ine—ine ndingakhale wosokonezeka. Izo zikanandipangitsa ine kukhala wamanjenje kwambiri, ine sindikanadziwa zomwe ine ndinali kuchita. Mukuwona? Ndipo ine sindingadziwe komwe ndingawauzire anthu, “Chabwino, tsopano, Iye adzachita *izi*, kapena Iye adzachita *izo*.” Ine—ine sindikanakhoza kukuuzani inu. Ine sindikudziwa. Koma pamene inu mukudziwa zimene Iye analonjeza Iye akanadzachita, ndipo mwamuwona Iye akuchita *izo*, ndiye inu mukudziwa pamene inu mwaima. Mukuwona? Ndipo onani momwe Mulungu, mu dongosolo Lake lalikulu, ankangodziwa momwe angamupangire munthu aliyense ndendende basi kuti akhale chinthu chinachake, chifukwa Iye adzawagwiritsa ntchito iwo kwa cholinga chimenecho.

15 Inu munamumva dona wamng’ono uyo kuno, kanthawi kapitako? Akazi a Stricker, akuyimba popanda nyimbo iliyonse. Iye anali ndi mtundu wina wa kanthu kakang’ono kamene iye amawuziramo, kuti apeze nyimbo yake, pake—poyambira pake kapena chirichonse chimene inu mumachitcha icho. Ndipo amakhoza kuyima ndi kuyimba ndi liwu lotsika kwenikweni ilo, ndi kumalikweza ilo mmwamba, ameneyo, *Ship Ahoy!* Tsopano, inu muyenera kudzandimva ine ndikuyesera izo nthawiina. Izo zingakhale zoipa. Koma, inu mukuwona, Mulungu ankadziwa basi momwe angamupangire mkazi ameneyo kuti azichita zimenezo.

16 Ndipo ndiyo njirayo. Ife tonse tiri ndi mapangwidwe osiyanasiyana. Ngati ife tikanangopeza malo athu mwa Khristu, ndi kukhala pamenepo ndi kumutumikira Iye.

17 Onani msungwana wamng’ono wakhala apa, mmawa uno, mu chikuku. Adalitse mtima wako wawung’ono. Chakulumalitsa iwe ndi chiyani, wokonedwa? Muscle dys-. . . dys-. . . O, ine sindingathe kunena mawu amenewo, pamene ine ndinayamba; dystrophy, kapena chiyani. Kodi ndi zomwe izo ziri, wokonedwa, zomwe zakupanga iwe kukhala wolumala, kapena ndi poliyu? Poliyu. Inu mukudziwa, Yesu amachiritsa atsikana aang’ono. Sichoncho Iye? Ndiwe msungwana wamng’ono wokongola kwambiri. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Yesu akulola iwe kuti ukhale bwino.

18 Usiku watha, asungwana aang’ono awiri awo omwe anakhala pano ndi nthenda imeneyo amene ngakhale munthu pa dziko lapansi samadziwa chimene icho chiri. Zala zawo zazing’ono zitagwa, ndipo mapazi awo aang’ono atagwa. Atsikana awiri okongola. Ndipo ine ndinapezeka kuti ndikuwadziwa amayi awo ndi agogo awo aakazi.

Ndipo ndinangomverera kutsogozedwa kuti ndimudzudzule mdierekezi ameneyo amene amazonza tinthu tating'ono tija titakhala pamenepo; kunja komwe. Ndipo iwo akhala ali mu zikuku kwa ine sindikudziwa kuti kwanthawi yayitali bwanji. Ndipo usiku watha, nkhani inabwera monsemo, pa telefoni, "Atsikana aang'onowo adzuka, akuyendayenda." Inu mukuwona izo, kuti—kuti Ambuye Mulungu anali wachisomo kwambiri kwa iwo. O, Iye ndi wabwino kwambiri kwa ife! Ife tiyenera kumuyamikira Iye kwambiri.

¹⁹ Ndiye ine ndinali kuganiza, usiku wangothawu, ine nditapita kunyumba ndipo nditagona kwa maminiti pang'ono, Ine ndinali kuganiza za, "Pamene solo yatuluka mwa munthu, ndi chiyani icho?" Ndi umunthu wake wamkati womwe watuluka. Iye sanafe. Iye—iye akadali wamoyo. Mukuwona? Iye—iye ali ndi moyo kosatha. Ndipo okonedwa athu amene adutsa kupyola chopimba ichi, ali mu—thupi lomwe ife sitikulidziwa chomwe ilo liri. Ilo silinawululidwe.

²⁰ Pali magawo atatu a chirichonse. Pali gawo la thupi lachivundi, thupi lachisavundi, ndipo kenako thupi laulemerero. Mukuwona? Basi monga zinthu zina, monga. . . Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera, amapita mu njira imodzi, ndipo atatuwo amapanga Mmodziyo. Kulungamitsidwa, kuyeretsewa, ubatizo wa Mzimu Woyera, mu mpita, zimapanga mmodziyo. Ndiye, ndipo solo, thupi, ndi mzimu, zimapanga chimodzi. Ndipo zimayenda mu zitatu, ndipo zitatu ndi chimodzi. Ndipo tengani a—galasi la nsonga zitatu ndi kuliyika ilo padzuwa, ilo linyezimiritsa mitundu yake, komabe, mitundu seveni idzabwera kudzapanga umodzi.

²¹ Ndipo inu mutenge chofiira, ndi kuyang'ana kupyolera mu chofiira pa chofiira. Ndi angati akudziwa mtundu womwe uti udzakhale? [Osonkhana akuti, "Choyera."—Mkonzi.] Choyera. U-nhu. Kodi izo sizachilendo? Kuti, chofiira kudzera mu chofiira, chimawoneka choyera. Chofiira ndi chizindikiro cha chiwombolo. Ndipo pamene inu. . . Mulungu amayang'ana pa machimo athu ofiira, kudzera Mmagazi ofiira a Mwana Wake wofunika, iwo ali oyera. Kotero, koma, Iye ayenera kuyang'ana kudzera Mmagazi. Ngati sichoncho, iwo ndi ochimwa. Kotero ife tiyenera kukhala pansu pa Magazi.

²² Ndipo pamene solo ichoka mu thupi, iyo imayenda ulendo wake kupita kumalo opumula, mu thupi lomwe liri mmawonekedwe ndi mapangidwe a thupi ili, koma ilo si mtundu uwu wa thupi. Inu mudzakumana ndi okonedwa anu. Inu simungathe kuwagwira iwo chanza. Inu mukhoza kuyankhula kwa iwo, inu mukhoza kuyang'ana pa iwo. Iwo amawoneka ngati momwe iwo amawonekera kuno. Chifukwa, pamene Petro, ndi Yohane, ndi Yakobo, anawona Mose ndi Eliya, iwo anawazindikira iwo, pa Phiri la Chiwalitsiro. Koma, ndi thupi.

²³ Koma ndiye pamene thupi limenero, lokhala ngati thupi lauzimu, pamene ilo likubwerera ku dziko lapansi, ilo limanyamula—chinthu chimene ilo poyamba linkakhalamo, ndipo kenako ilo limasandulika thupi laulemerero. Ndipo thupi limenero ndi limene ife tidzawawona Ambuye Yesu, mu thupi Lake lowukitsidwa. “Izo sizimawonekabe chomwe ife titi tidzakhale,” anatero Paulo, “koma ife tikudziwa ife tidzakhala nalo thupi longa thupi Lake lomwe laulemerero, pakuti ife tidzamuwona Iye monga Iye aliri.”

²⁴ Ndipo manja onse akale amakwinya awa ndi minyewa yoswekayi zonse zidzazimirira mu kukongola kwa unyamata. Inu amuna achikulire ndi akazi, kumbukirani, inu...Izi ndi...Icho, ndicho chizindikiro cha kugwa, ukalamba wanu. Koma mu chiwukitsiro, iwo sadzakhala chizindikiro chimodzi cha chirichonse cha tchimo. Koma ndi chifukwa chiyani Mulungu anakupangani inu monga mmene Iye anachitira? Iye anakufikitsani inu ku usinkhu winawake, pamene inu munali pafupifupi twente-thuu, usinkhu wa zaka twente-firii, inu munali pachimake chanu. Inu munali mukudya chakudya ndi kumakhala wamphamvu, ndi wathanzi, ndipo inu munali munthu wowoneka wamphamvu bwanji. Ndiye, zitatha izo, inu munakhala wamakwinya, mwawona, imfa inalowamo. Koma, mu chiukitsiro, ukalamba wonse udzafafanizidwa.

²⁵ Ine ndikuyang’ana kuno pa mlaliki wamng’ono wachikulire ndi mkazi wake. Iwo ali mu zaka zawo za mmaeyite, ine ndikuganiza. M’bale ndi Mlongo Kidd, akulalikira Uthenga mwinamwake ine ndisanabadwe; ndipo ndine bambo wachikulire. Ndipo ine ndikuwawona iwo atakhala apa, owoneka mwamtendere, banja laling’ono lachikale. Ndipo ine ndikungoganiza, kuti, mu chiukitsiro, momwe iwo ati adzawonekere. Makwinya akale awo, ndi kugwedezeke kwa manja onjenjemera ndi kulumala, ndipo tsitsi laimvilo lidzazimirira mu kukongola kwa unyamata. Iko kumapindulitsa kwenikweni kumutumikira Ambuye. Iko kumaterodi. Ife tidzamuwona Iye, tsiku lina.

²⁶ Ndikudabwa ngati Rosella Griffin alipo. Ine ndikufuna kuti iye anene mawu. Chidakwa wamng’ono yemwe anachiritsidwa kumene pa...kuno, zaka zingapo zapitazo. Ndipo izo zitha kuthandiza chidakwa wina yemwe ali pano. [Mlongo wina mumpingo akuti, “M’bale Branham, iye wapita kwawo mmawa uno.”—Mkonzi.] Anayenera kuti apite kwawo mmawa uno. Chabwino. Nkhani yodabwitsa! Ine ndinaganiza usiku watha ndikanamuza iye kuti anene chinachake. Ine ndikanatero, ngati ine ndikanadziwa izo, kuti iye anali kupita mmawa uno. Zinthu zambiri zomwe ine ndimangokonda anthu amkachisi kuti azimve.

²⁷ Tsopano, kodi alipo aliyense pano woti abatizidwe, mmawa uno, mmadzi? Tiyeni tiwone. Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi,

pafupifupi sikisi kapena seveni pano kuti abatizidwe. Ndipo utumiki waubatizo udzatsatira phunziro la Sande sukulu ili.

²⁸ Tsopano, chipinda cha Sande sukulu cha Mlongo wathu Arnold, cha ana ake aang’ono, chadulidwa. Ndipo ife tidzangoti, ngati inu mungatero, Mlongo Arnold, ife tingotsala pang’ono kuti tilepheretse izo mpaka tsiku lotsatira, chifukwa ife tiribe chipinda cha sukuluyo. Ndipo ine ndiwerenga Lemba lina apa mmaminiti pang’ono, kwa ana aang’ono, ndipo izo zidzawapatsa iwo chinachake choti achiganizire, nawonso. Ndiyeno Lamlungu likudzali inu mudzapatiriza ndi misonkhano yanu yachizolowezi ndi Sande sukulu. Tsopano, ife tikufuna kuti tinene. . .

²⁹ Apa pali chinthu china chimene ine ndikufuna kuti ndinene mmawa uno. Ine—Ine—Ine ndinawauza iwo kuti asachite izi, koma iwo anachita izo, mulimonse. Mukuwona? Icho chinali, chopereka usiku watha chimene chinabwera kwa ine, mwawona, chopereka. Ine ndinawauza iwo kuti asachite zimenezo, mwawona. Ndipo iwo. . . Koma iwo anachita izo, mulimonse. Ndipo pamene. . . Ine sindimadziwa izo kufikira Billy anandiua ine kuti m’bale wanga Doc anali atabweretsa icho kwa iye, kunyumba kwake. Ndipo ine sindinaziwerengebe izo, koma ine ndikukhulupirira kuti izo zinanenedwa kuti panali pafupifupi firii handiredi, kapena kupitirira pang’ono firii handiredi. Ndi zimenezo. . . Inu mukukumbukira, Doc, chomwe icho chinali? [M’bale Edgar Branham akuti, “. . . twente-foro, thwelofu.”—Mkonzi.] Chinali chiyani icho, m’bale? [“Firii, twente-foro, thwelofu.”] Firii handiredi ndi twente foro, thwelofu. Ine ndikukuthokozani inu, mochuluka kwambiri.

³⁰ Tsopano, ine ndakhala ndikupuma pa ntchito kwa nthawi yayitali. Inu mukudziwa zimenezo. Ndipo mlembi wanga pokhala alipo, kapena ena a iwo pano mmawa uno, akudziwa kuti zolipira zanga, ziribe kanthu komwe ine ndiri, komwe kuno kunyumba, zimanditengera ine kupitirira madola handiredi patsiku, za maofesi anga ndi zinthu zoti ndizitengere mipango ndi zinthu kuzungulira dziko, mu ndalama.

³¹ Ndipo ine—ine ndikufuna kuti ndinene izi, chilimbikitso kwa inu anthu kuno, ngakhale. Kwa kuchuluka kwa anthu, ndicho chopereka chochuluka kwambiri chimene ine ndinayamba ndalandirapo mmoyo wanga. Kodi inu mukuzindikira kuti izi zitha kukhala pafupifupi dola imodzi chidutswa, pafupifupi? Ndipo zambiri mwa zopereka zonse zoperekedwa mu ntchitoyo zizikhala pafupifupi, pafupifupi masenti twente thuu kapena twente faivi pa munthu. Koma ichi chinali pa pafupifupi dola pa munthu. Chifukwa, ine ndikudziwa inu simungakhoze kulowa muno. . . Iwo samatengera zopereka kunja. Ndipo inu simungakhoze kupanikizana mmalo aang’ono awa, pafupifupi anthu firii handiredi, ine—ine ndikukayikira. Kodi inu mukudziwa anthu omwe angakwane mu kachisiyu, M’bale Neville? [M’bale Neville akuti, “Izo

ziyenera kukhala penapake mozungulira firii handiredi, momwe izo ziliri tsopano.”—Mkonzi.] Pafupifupi anthu firii handiredi. Kotero, onani, izo ziri mozungulira a—dolla chidutswa. Mulungu akudziwa momwe ine ndikuyamikirira izo. Ine ndikukuthokozani inu mochuluka kwambiri. Ndipo izo zimapita molunjika kumene mu ntchito ya Ambuye. Ine—ine ndikukuthokozani inu chifukwa cha izo. Ndipo kwa . . . Ngati ena a iwo akanati azichoka usiku usanafike, chifukwa . . . ndipo ine . . .

³² Pamene ine ndinapita kunyumba usiku watha, nditakhala pa khonde panali bokosi laling’ono, monga *chonchi*, ndipo ilo linali a—mulu wa mafuta, Ine ndikukhulupirira, iwo anachokera kwa winawake. Inu mukudziwa, ine ndimangokonda mafuta. Ndipo ine—ine ndikuyamikira zimenezo. Ndipo a—mlongo pano, yemwe ine kulibwino ndisamutchule dzina lake. Iye ndi bwenzi lapamtima la banja lathu, ndipo iye anasiya mphatso yachikondi kwa amayi anga, ya ine ndi Billy. Inu simukudziwa, mlongo, momwe ine ndikuyamikirira izo, ndipo ndinthawi yotani yomwe izo zimabweramo.

³³ Ndipo, o, zinthu zochuluka kwambiri! Inu mukumvetsa. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti Iye akumvetsa. Ndipo kotero ine ndikungodalira kuti Iye adalitsa aliyense wa inu, mopitirira kwambiri. Ine ndikanakonda izo zikanakhala choncho kuti ine ndipite kunyumba ndi mmodzi aliyense wa inu, ndi—ndi kukhala ndi inu kanthawi pang’ono, ndi kuyankhula ndi inu. Ine ndimakonda kuchita zimenezo.

³⁴ Koma, ziri, inu mukudziwa momwe izo ziliri, izo zimangokhala pa chochitika. Ife tiyenera kuti tizipita mofulumira. Mosabisa, ukangotha msonkhano usikuuno, Ambuye akalola, ine ndichoka mu chigawochi, mwamsanga basi msonkhanowu ukangotha. Ine ndikuyenera kutuluka muno isanakwane thwelofu koloko. Ine ndiri ndi zokambirana nthawi ya thwelofu koloko. Ndipo ine ndiri nazo zodzadza, madzulo ano. Ndipo ine . . . Inu mukudziwa momwe izo ziliri. Izo zimangokhala kawirikawiri poyambirira, nthawi zonse; anthu akudwala, akufa.

³⁵ Ndipo nthawi zambiri ine ndimapita ku malo, ndi kumangokhala nditayima pamenepo, ndipo wina amalowa mkati, nati, “Inu mukundidziwa ine, M’bale Branham?”

“Ayi, ine sindikutero.”

³⁶ “Bwanji, ine ndinali kugona mu chipatala, ndikufa, pamene inu munabwera kudzandipempherera ine. Ambuye anandichiritsa ine.” “Ine ndinali wakhungu pamene inu munakumana nane ine pa njira, tsiku limenero kuwona anabwera.” Mukuwona? Ndipo ine—ine sindimadziwa chomwe icho chinali.

37 Koma ine ndikuganiza lingaliro limodzi lodala ili, M'bale Egan, kuti, tsiku lina pamene ine ndalalikira ulaliki wanga wotsiriza, Ine ndapempherera munthu wotsiriza yemwe Ambuye akufuna kuti ine ndimupempherere, ndipo ine ndikupita Kwathu! Ndipo pa mmawa wa chiukitsiro uwo, o, lidzakhala tsiku lotani ilo, chimwemwe! Pamene ine ndingakhoze kudzayima Pamenepo, pamene mfumukazi ya Kummwera idzabwerapo, ine ndikukhoza kuwona kukopa komwe iyo inali nako! Ine ndidzamuwona akubwera Apo, Billy Graham, kukopa komwe iye anali nako. Oral Roberts, ndi ena onse, a Sankey, Finney, Moody, Calvin, Knox, ndi ena otero. Kenako ndidzawona gulu langa likubwera. O, chimenecho chidzakhala chimwemwe, uko kudzakhala kuvekedwa korona kwanga. Uko nkulondola. Ndipo, mwa chisomo cha Mulungu, ine ndikuyembekeza kudzakhala nawo mamiliyoni angapo Kumeneko.

38 Ndipo tsopano ine ndiyenera kupita kutsidya kwa nyanja posachedwa kwambiri. Ndipo tsopano, monga momwe ine ndikudziwira, mmisonkhano yathu yomwe ino, tangoganizani za izo, ine ndiri mmiyoyo yanga miliyoni yachiwiri, kupindulira kwa Khristu. Ndipo ine—ine ndikuyembekeza kuti ine ndikuwona ambiri, mamiliyoni ambiri ndawapindulira.

39 Tsopano, utumiki wa ubatizo, ndipo tsopano zo—zokambirana ndi zinthu. Ndipo, tsopano, izi ziri mopitirira ukatha msonkhano.

40 Ngati nthawi iliyonse yomwe inu mukubwerera ku zokambirana zapadera, kapena zina zotero, ingomuyimbirani wothandizirayo, M'bale Mercier kuno. Ife tikuyenera kukhala ndi mtundu wina wa machitidwe, omwe ife tikuyenera kutero. Ife tikudziwa zimenezo. Ndipo M'bale Mercier, iye amazilemba izo, iye amazilemba izo basi pamene izo zikubwera, ndipo mwamsanga pamene zokumana zandithera ine, zonse za izo zatha, ine... Pamene ine ndilowa, ine ndimamuyitana ndikumuuza iye kuti, "Ine ndamalaza pagulu limenero." Iye amandipatsa ine gulu latsopano, ndipo kutali ine ndimapita kachiwiri, inu mukuwona. Ndiye, zonse zimagwira ntchito kuchokera mu ofesi imeneyo. Ndipo iye amadziwa basi momwe angawakhazikitsire iwo kotero kuti iye akhoze kumulowetsa aliyense mkati, yemwe angakhoze kulowamo, inu mukuwona. Kotero, ndife okondwa kukhala ndi ofesi yaying'ono iyi ikugwira ntchito momwe iyo ikuchitira. Kotero ndiyo basi BUTler 2-1519. [Nambala yafoni yasinthidwa.—Mkonzi.] Ndipo ndizo... Kapena, ngati inu mukuyimbira ku Jeffersonville, mungondiyimbira ine, ndipo iwo adzayankha kumeneko ku ofesi imeneyo. Ndipo zikomo inu, mokoma mtima kwambiri.

41 Tsopano tiyeni ife, ife tisanati titsegule Mawu Ake odala... Ndipo kumbukirani, mwamsanga msonkhano uwu ukangotha,

ndi utumiki waubatizo, Billy akhala pano kuti apereke makadi apemphero a usikuuno.

⁴² Tsopano, usikuuno pokhala usiku wa mpingo, Lamlungu usiku, ochuluka a anthu a mu mzinda adzakhala ali kunja mmipingo yawo yomwe, ndi mozungulira Louisville ndi kuzungulira. Iwo adzakhala mmipingo yawo yomwe. Koma iwo adzakhala makamaka akunja. Chotero, ine ndikuganiza mwinauwake ife tikhoza kufola mzere waukulu wa pemphero usikuuno ndi kupempherera aliyense wa iwo. Ine ndikudalira kuti ife tidzatero. Ife tiri nawo ndithu makadi apemphero ochepe.

⁴³ Ine—ine ndikuganiza, usiku watha, pambuyo pa usiku watha, o, ine ndinangomverera ngati ine nditenga imodzi ya izo, o, ndege yandekha, inu mukudziwa, ife timakambirana. Basi kungowona, mu kachisi wamng’ono wakale uyu, kachiwiri, manja atakwezedwa mmwamba.

⁴⁴ Ine ndiri ndi mnyamata wamng’ono pano, iye ndi mnyamata chabe, Joseph wamng’ono. Iye ali pafupifupi zaka zitatu. Ndipo pamene onse a iwo anali kufuula, ngati iye sanalumphe apo pomwe pakati pa kanjira ndi kuponyera manja awo mmwamba, ndi kuyamba kufuula ndi kutamanda Ambuye, pakati pomwe pa kanjira kunja uko! Ndipo ine ndikuganiza, mmawa uno, iye analowa mu izo ndi mlongo wake wamng’ono, ndipo anamuluma iye pa mkono, kotero ine ndinamuuza iye kuti kufuula kwake sikungachite bwino ngati iye achita motero. O, mai! Ana aang’ono awo, iwo akhoza kukhala pafupi kwenikweni ndi inu, sichoncho iwo? Chabwino, ndithudi, chomwe icho chinali, iye anangowona ena onse a iwo akuchita izo ndipo anaganiza kuti ndizo basi zomwe iye akuyenera kuchita, nayenso, ndipo mwina amatitsatira pambuyo pathu, momwe ife tinali kuchitira.

⁴⁵ Tsopano ife tiri nawo Mawu Ake ali otseguka apa. Tsopano tiyeni ife tingoyankhula kwa Iye za Izo. Tsopano basi a . . .

⁴⁶ Wokonedwa Mulungu, pamene ife tikubwera kwa Inu pakali pano, molemekeza, mwakachetechete, mwanzeru, ndi mwa chikhulupiriro, kukhulupirira kuti Inu mumamva ndipo muyankha pemphero. Chifukwa, ife tikubwera mu Dzina lokwanira-zonse ilo la Mwana Wanu, Ambuye Yesu, Yemwe ali Mmodzi wosalepherayo, ndipo anapereka lonjezo, kuti, “Ngati inu mudzapempha Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Ndiye ife tikudziwa kuti ife tilandira basi zomwe ife tikupempha, pakuti ife tikubwera mu Dzina Lake. Pakuti ife tiribe Dzina lina limene ife tingakhoze kukufikirani Inu, wamkulu, Yehova Mulungu wamphamvu. Ndipo ife tikubwera mu chisomo Chake, osati kuvomereza kuti ife tikuyenera chirichonse, koma chifukwa Iye watichitira ife chiwombolo, mwakuti Iye anatifera ife. Ndipo Iye anatetezera chifukwa cha machimo athu, ndipo ife tikumverera kuti ife

tikhoza kuima olungamitsidwa pamaso Panu, mwa imfa Yake. Icho ndicho chikhulupiriro chathu. Ndi kupempha osati chimene chingakhale choipa, koma chimene chingakhale chabwino kwa aliyense wa ife.

⁴⁷ Chotero, Ambuye Mulungu, yankhulani kwa ife kudzera mu Mawu Anu. Ndipo yankhulani kwa ife mu Liwu limenero, kuti ife tikakhoze kumvetsa ndipo tikadziwe basi momwe ife tingakhalire amuna ndi akazi abwinoko, anyamata ndi atsikana. Podziwa kuti chipata chachikulu kutaliko pa imfa, chimene, nthawi iliyonse mtima wathu upanga kugunda, ife timangoyandikira kugunda kumodzi pafupi ndi chipata chimenecho chomwe ife tonse tidzalowamo. Ndipo tsopano podziwa, kuti, ife titatha kukhala mmenemo, palibe mwayi umodzi kachiwiri kuti tichitenso kuyanjanitsa. Palibenso nkomwe kenanso kuti ife tingakhoze kukhala ndi mwayi uwu umene ife tiri nawo panopa. Ndipo osadziwa basi ife tidzadutsa liti mzere umenewo, O Mulungu, bwerani kwa ife mwamsanga ndipo mutibweretse ife ku zokhudzira zomwe ife tiyenera kukhala nazo, ndi kudziwa momwe tingafikire kwa Inu, ndi kudandaulira mlandu wathu pamaso Panu ndi kupempha chifundo. Perekani izi, Ambuye.

⁴⁸ Ife ndife anthu osowa. Ife ndife nkhosa, tikuitanira pa M’busa amene atitsogolere ife kupyola mmoyo, ndi kutsika mchigwa cha mthunzi wa imfa. Monga Davide, wakaleyo, anati, “Ine sindidzawopa pamene ine ndidzafika pa malo amenewo,” chifukwa M’busa adzanditsogolera ine kudutsa mmalo amenewo, mpaka mapazi athu adzakhazikika molimba pa Gombe la ulemelero limenero, kumene ukalamba ndi matenda ndi chisoni ndi imfa zidzatithawa ife, ndipo ife tidzakhala omasuka, Kumeneko, kwanthawizonse.

⁴⁹ Yankhulani, Ambuye. Wokonedwa wamng’ono wa winawake wa maso owala uyu, wakhala apa patsogolo panga, mu chikuku ichi; sindingakhoze kuchotsa maso anga kwa iye lero; yense wolumala ndi poliyo iyi, chimene woyipayo wachita kwa iye. O Mulungu, bweretsani chiwombolo kwa wokonedwa wamng’ono uyo. Perekani izi, Ambuye. Osati kwa iye yekha, komanso kwa ena pano amene akuyembekezera. Mulole Mzimu Wanu Woyera uwakweze iwo pamwamba kwambiri, mmawa uno, kuti adzadutse kugwedezeka kulikonse kwa chikaiko ndi chotchinga chirichonse cha uchimo, kuti Mzimu Wanu Woyera ukhoze kusuntha pa iwo ndi kuwachiritisa iwo. Perekani zinthu izi, Ambuye. Pakuti ife tikupempha madalitso awa kwa ulemmero Wanu, mu Dzina la Mwana, Yesu Khristu. Ameni.

⁵⁰ Tsopano, ine ndasankha kwa mutu mmawa uno. . . Ndipo inu ana aang’ono mundikhulukire ine, chifukwa chotenga nthawi yonse ndi akuluakulu, ndipo kalasi yanu palibe pano, sikhalapo mmawa uno. Koma ine ndikufuna kuti inu mumve, inunso, zomwe ine ndikufuna kuti ndiwerenge. Ndipo ine ndikufuna

kuti ndiwerenge, mmawa uno, kuchokera mu Samueli Woyamba, mutu wa 3.

⁵¹ Ndipo ine ndikufuna kutenga ngati mutu: *Imvani Liwu Lake*. Izo zidzachita kwa asungwana aang'ono ndi asungwana aakulu, ndi anyamata aang'ono ndi anyamata aakulu, onse. Kumbukirani mutuwo: *Imvani Liwu Lake*.

⁵² Tsopano, inu amene mukutembenezira Mmalemba, ku Samueli Woyamba, mutu wa 3, umu ndi mmene akuwerengekera kwa ndime teni zoyambirira.

Ndipo mwanayo Samueli anatumikira AMBUYE pamaso pa Eli. Ndipo mawu a AMBUYE anali a mtengo wapatali mmasiku amenewo; panalibe masomphenya otseguka.

⁵³ O, momwe ine ndikanafunira kukhala pamenepo kwa miniti, mwinamwake nthawi ina. Izo zimangondikhuza ine. Ndiloleni ine ndingowerenga izo kamodzinso, ndime imeneyo.

Ndipo mwanayo Samueli anatumikira AMBUYE pamaso pa Eli. Ndipo mawu a AMBUYE anali amtengo wapatali mmasiku amenewo; pakuti panalibe masomphenya otseguka.

⁵⁴ Mukuwona chomwe masomphenya ali, ndiye? Ndi Mawu achindunji a Ambuye. Mukuwona? Ndipo Mawu a Ambuye anali a mtengo wapatali.

Ndipo zinachitika kuti nthawi imeneyo, pamene Eli anali atagona mmalo ake, ndipo maso ake anayamba kuchita mdima, mwakuti iye samakhoza kuwona;

Ndipo nyali ya Mulungu inazima mu Kachisi wa AMBUYE, kumene kunali likasa la Mulungu, ndipo Samueli anaikidwa pansu kuti agone;

Kuti AMBUYE anamuitana Samueli: ndipo iye anayankha, Ndine pano.

Ndipo iye anathamangira kwa Eli, ndipo anati, Ndine pano; pakuti inu munandiitana ine. Ndipo iye anati, ine sindinaitane; kagonenso pansu. Ndipo iye anapita ndipo anakagona.

Ndipo AMBU-...Ndipo AMBUYE anamuitananso, Samueli. Ndipo Samueli anadzuka ndipo anapita kwa Eli, ndipo anati, Pano ndiri...Ndine pano; pakuti inu munandiitana ine. Ndipo iye anayankha, ine sindinakuitane, mwana wanga; kagonenso pansu.

Tsopano Samueli sanamdziwe apobe AMBUYE, ngakhale mawu a AMBUYE sanavumbulutsidwebe kwa iye.

Ndipo AMBUYE anamuitananso Samueli kachitatu. Ndipo iye ananyamuka ndipo anapita kwa Eli, ndipo

anati, Ndine pano; pakuti inu munandiitana ine. Ndipo Eli anazindikira kuti AMBUYE anamuitana mwanayo.

Chifukwa chake Eli anati kwa Samueli, Pita, ukagone: ndipo kudzakhala kuti, ngati iye akuitana iwe, iwe udzati, Yankhulani, AMBUYE; pakuti kapolo wanu akumva. Choncho Samueli anapita ndi kukagona mmalo ake.

Ndipo AMBUYE anadza, ndipo anaima, naitana monga nthawi zinazo, Samueli, Samueli. Ndipo Samueli anayankha, Yankhulani; pakuti kapolo wanu akumva.

⁵⁵ Liwu la Mulungu! Kumva Liwu Lake mu tsiku limenero chinali chinthu chosowa. Mwawona, apo panalibe masomphenya otseguka. Ndipo icho chinali chinthu chosowa, Liwu lenileni la Mulungu, chifukwa anthu anali atapita kutali. Iwo anali nawo mpingo, mu tsiku limenero, umene sunali basi kutsatira malamulo a Ambuye. Iwo anali ndi m—mtumiki dzina lake Eli. Ndipo iye anali atachoka kwa Mulungu, pa kungophunzitsa malangizo a zimene anthu ankafuna kuti azizikhulupirira. Ngati izo sizikufanana mpaka tsiku lalero! Iye ankangowaphunzitsa anthu, ndipo iye—iye anatenga osankhidwa ake, ndipo iye anapatsa ana ake aamuna kuti atenge nyama yabwino koposa mmenemo, mbedza, kuchokera mu—mu chopereka. Ndipo iwo anangosanduka malo omwe chopereka chinali chinthu chachikulu. Ndipo Samueli, basi wasamala za momwe iye anachitira ndi malamulo a Ambuye. Ndipo Mawu enieni a Mulungu anali chinthu chosowa.

⁵⁶ Umo ndi momwe izo ziliri lero. Ife timapita ku tchalitchi ndipo ife timapeza anthu akulowa mkati ndi kumakhala ndi kuyendetsa kwakukulu, “Ife tikufuna kupanga chipembedzo chatu, chaka chino, *ochuluka* kwambiri ena. Bweretsani kalata yanu kuchokera ku mpingo wanu wina, ndipo mulumikizane ndi ife.” Ndipo mitu monga, “Miliyoni owonjezera mu ’44.” Ndi zonse monga izo, kufuula, kuyesera kuti ukule kuposa chipembedzo chotsatira. Ndipo pochita zimenezo, tasiya zigwiriro, za Baibulo. Ife tachoka, ndipo tayamba kuphunzitsa zinthu zosiyana.

⁵⁷ Aneneri anayankhula za masiku ano, kuti pamene, “Iwo, pakuphunzitsa, adzaphunzitsa chiphunzitso cha munthu osati Chiphunzitso cha Mulungu.”

⁵⁸ Ndipo ife tawona zochuluka kwambiri za izo, ndipo izo zapitirira motalika kwambiri, mpaka, lero, Mawu a Ambuye ndi chinthu chosowa, kuti wina akhoza kubwera ndi kunena, “PAKUTI ATERO AMBUYE.” Tsopano, ife takhala nazo zotsanzira zambiri za izo. Satana alidi pa ntchito. Ndipo zaka zambiri zapitazo, anthu ankachita mantha kunena zimenezo pokhapokha anali Ambuye. Koma, lero, iwo samasamala basi. Koma ndi chinthu chosowa kumva Liwu la Ambuye, ndi kupeza

munthu amene angakhoze kunena, “Ambuye anayankhula kwa ine.” Inu mumazindikira zimenezo pakati pa anthu, panonso, kuti iwo samamva nkomwe nthawi yomwe iwo amati, “Ambuye anayankhula kwa ine.”

⁵⁹ Pamene, amuna ndi akazi anali kupemphera usiku wonse, ndipo nyumba zawo zinkaikidwa mu dongosolo, mwa Bukhu la Ambuye, ndipo Mulungu anali woyamba mnyumba mwawo.

⁶⁰ Mwawona, ife tiri nazo zinthu zochuluka kwambiri patsogolo pa Ambuye. Inu simungakhoze kukhala ndi msonkhano wa mapemphero, chifukwa Bambo Godfrey alipo usikuuno. Inu simungakhoze kukhala ndi msonkhano wa mapemphero, chifukwa *We Love Sucky* ilipo usikuuno. Kapena, mtundu wina wa zamkutu zopusa ngati zimenezo, zomwe zimatenga nthawi, ndipo ife tiribe nthawi yoti timve Liwu la Ambuye. Ndipo iwo amene amadzinenera kukhala Akhristu, amangogwada pansi, pa pemphero laling’ono monga ili, lokhala ngati lopangidwa kunyumba, “Ambuye, ndidalitseni ine ndi banja langa, ndipo mutisamalire ife. Usiku wabwino.” Ndipo m’mawa wotsatira, kudzuka ndi kunena, “Mungotilondolera ife kudutsa tsikuli. Tsiku labwino.”

⁶¹ Ife tiyenera kuyembekezera pa Ambuye. Inu mukuwona, ife timapanga kuyankhula konse. Ife sitimamupatsa Iye mwayi woti ayankhule kwa ife. Kuti, ngati ife tikanati tipemphere, ndi kupemphera mpaka moyo wathu ubwere mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndipo kenako nkungomasuka ndi kumvetsera ku Liwu Lake.

⁶² Koma pali maliwu ochuluka, lero, amene amatengera Liwu la Ambuye kutali ndi ife. Pali liwu la zosangalatsa. Anthu ambiri amamvetsera ku ilo, kumene iwo angakhoze kupita ndi kukakhala ndi nthawi yabwino. Ndipo ambiri a iwo akudzinenera kukhala Akhristu. Mtundu wina wa gwedemula wakale ukubwera, iwo sangakhoze basi kumvetsera ku chimene chaumulungu. Iwo amati, “Chabwino, ndine Mkristu, ine ndiyenera kuwerenga ndime mu Baibulo lero. Inde, ‘Yesu analira.’” Ndi zimenezo. Pitirirani. Koma ndiye kuti atsike pansi kwenikweni ndi kupemphera, iwo ali nazo zinthu zina zambiri zoti achite. Pali maliwu ambiri mdziko lapansi, zinthu zambiri zokopa tcheru chathu kuchoka kwa Mulungu.

⁶³ Ndipo dzulo, pamene mkazanga ndi ine tinathamangira ku malo ogulitsira, kuti tikagule zina zapanyumba. Ndipo ine ndinali kufulumira chifukwa ine ndinachedwa ndi zokumana ndi zinthu, ndi kuthamangira mwamsanga kwenikweni. Ndipo apo panali mnyamata wamng’ono atayima pamenepo, ali pafupi kugona, ndipo msungwana wokulirapo pang’ono anabwera pamenepo atavala thalauza lina laling’ono, limene linali la mwamuna wina. Iwo ankayenera kutero, chifukwa iwo anapangidwira mwamuna.

64 Ndipo Baibulo limati, “Ndi chonyansa pamaso pa Mulungu, kuti mkazi azivala izo.”

65 Ndipo ali ndi zambiri za izi apa zopaka mmilomo, ndipo maso ake ali pafupi kugona, iye anati, “Ali kuti *wakuti-ndi-wakuti*?” kwa mnyamata wamng’ono uyo.

Iye anati, “Iwe ukuyembekezera kuti ine ndidziwa bwanji?”

66 Iye anati, “Iwe ukukumbukira, ine sindinalowemo mpaka sikisi koloko mmawa uno.” Ndipo iye anali asanadutse zaka thwelofu.

67 Tsopano, Yesu, pa thwelofu, chimene chinali chitsanzo chathu, anati, “Kodi inu simudziwa kuti Ine ndiyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?”

68 Nzosadabwitsa Liwu la Mulungu ndi chinthu chosowa lero. Ilo lazimitsidwa, ndi maliwu ambiri osiyanasiyana, zinthu zambiri zomwe zimalizimitsa ndikulichotsa. Izo zafika pa malo mpaka izo zimafoola zokhudzira zathu, mpaka ife sitingakhoze kumva Liwu la Mulungu. Zokhudzira zathu, za komwe ife tiyenera kudzigwedezeka tokha, ndipo zindikirani kuti inu ndinu amuna ndi akazi, ndipo inu ndinu zolengedwa za Mulungu, ndipo inu munaikidwa pano kuti muzimutumikira Iye. Koma liwu la Satana ndi aneneri onyenga, “O, khalani amakono!”

69 Pamene ine ndinali kuyankhula masiku angapo apitawo, ine ndinali kubwera ku tchalitchi, ndipo ine ndinayatsa walesi yanga. Ndipo ine ndinamva purogalamu kuchokera ku Louisville, imene inanena kuti iwo anali kuphunzitsa ana awo, mmatchalitchi, kuti azingomwako mwapang’ono. Kuwapanga iwo kukhala amakono, kotero kuti iwo asapite mopitirira malire.

70 O, iwo akuyenera kuwaphunzitsa iwo Khristu, osati kumwa. Ndipo izo zidzaphwasula ndi kuwononga ndi kuwononga nyumba iliyonse. Liwu la Mulungu lingakhoze bwanji kuyankhula pakati pa banja lomwe lakhuta pang’ono ndi kachasu, ndipo malingaliro awo atapuwala ndi kusuta ndi kumwa, ndi kusangalala kwa usiku wonse?

71 Anthu amene akuyembekezera pa Mulungu, amabwera mu Kukhalapo Kwake. Ndipo kubwera mu Kukhalapo kwa Mulungu kuli ngati kutuluka m’bandakucha, pamene mame ndi udzu zonse ziri zokoma. Pamene inu mubwera mu kukhalapo kwa munthu wotero, inu mumadziwa kuti iwo akhala ali ndi Mulungu.

72 Mkazi wanga ananena kwa ine, ndikubwera kuno, mmawa uno. Iye anati, “Billy, ine sindikutanthauza kuti ndinene izi kuti ndipereke maluwa kwa aliyense. Koma,” iye anati, “usiku watha,” ine ndikukhulupirira, kapena umodzi wa mausiku, iye anati, “Ine ndinakhala pafupi ndi mmodzi wa akazi aang’ono Achiamishi, ndi dona wamng’ono ali ndi chipewa chaching’ono pamutu pake.” Iye anati, “Ndipo inu mukhoza kudziwa kuti

mkaziyo anali ndi Yesu, pakuti iye anali wokoma. Moyo wake unali wodekha. Maso ake anali oyera.” Palibe tchimo kapena chirichonse chobisala kumbuyo, kapena chirichonse. Iye anali ali mu Kukhalapo kwa Mulungu. Zokhudzira zake sizinali zofooka, ndi kachasu ndi fodya, ndi mitundu yonse ya zinthu za mdziko. Iye anatsitsimutsidwa kuchokera mu Kukhalapo kwa Mulungu, kuwerenga Baibulo lake, kuphunzira Mawu a Mulungu.

⁷³ Koma, ife Achimereka amakono, zomwe ife timachita! Ndipo aneneri abodza kuseri kwa guwa amati izo nzabwino. Ndiri ngati wosakhazikika kunena izi. Ngati ine ndikulakwitsa, Mulungu andikhululukire ine. Ine ndikukakamizika kuti ambiri a iwo samamuziwa Mulungu. Ndipo osonkhana sadzakhala konse momo wapamwamba kuposa abusa awo. Nzosadabwitsa Lemba limati, “Abusa awa, momwe iwo abalalitsira gulu lankhosa! Tsoka kwa iwo. Iwo ndi nthambi zimene sizibala zipatso, zimene zidzadulidwa ndi kutenthedwa.”

⁷⁴ Zinthu zambiri zoti zifoole zomverera za anthu lero! Oh! Koma mkati mwa zonsezo, pambali pa kufooka kulikonse ndi liwu lililonse lomwe liri padziko lapansi lero! Ena a iwo, maliwu a zosangalatsa. Ena a iwo ndi—ndi maliwu auchimo, kuti akope anthu. Koma pambali pa kachidutswa kalikonse ka izo, Choonadi cha Mulungu chidakalipobe, “Iye amene ati adzamve Liwu Langa nanditsata Ine!” Amuna ndi akazi amene adzamva Liwu la Mulungu: Mulungu akuyembekezerabe kuyankhula ndi munthu aliyense amene ati adzatsegule makutu awo kuti amve Liwu la Mulungu.

⁷⁵ Ngati munthu, yemwe iye ali, ndi m’busa . . . Nthawi zambiri, anthu amati, “Kodi inu simukanakhoza kuchita *izi*? Kodi inu simukanakhoza kuthamangira *kuno*? Kodi inu simukanakhoza kuchita *izi*?” O, ine ndimakonda kuchita izo. Koma ine ndiyenera kukhala mu Kukhalapo kwa Mulungu ngati ine nditi ndichite chinthucho molondola. Kenako anthu amati, “O, M’bale Branham ndi mmodzi wa odzipatula awa.” Izo si zimenezo. Ine ndimakonda anthu, koma basi pali masauzande a iwo. Koma ine ndimayenera kukhala ndi Iye, kuti ndipeze chimene Iye angati ine ndiwawuze iwo. Penapake, ingomvetserani, Iye adzakhala nacho chinachake cha inu, chimene Iye akufuna kuti inu muchidziwe.

⁷⁶ Abusa, musati mukhale otanganidwa kwambiri koma chomwe inu mungakhoze kukhala mu Kukhalapo ndi kumvetsera Liwu Lake. Mulungu nthawizonse amasunga Mawu Ake. Ndipo ziribe kanthu momwe nthawi zingakhalire zoipa, mochuluka bwanji momwe mpingo wanu ungaphunzitsire motsutsa izo, Yesu Khristu akadali wololera kuti ayankhule Liwu laling’ono limenero kwa aliyense amene angamvetsere kwa Iye. Iye akadali wokonzeka kuti achite izo, ngati ife tingangodzitontholetsa tokha.

77 Koma ife timathamangira mkati, mokhumudwa, ndi kuti, “Mukuti, abusa, kodi ine ndingajowine mpingo uno?”

“Kodi mumachokera mpingo uti?”

“*Wakuti-ndi-wakuti.*”

“Chabwino, tibweretsereni ife kalata yanu.” O, mai!

“Kodi ine ndingajowine mpingo uwu?”

78 “O, inde. Bwerani, ndipo tidzakukonkhani inu pang’ono, ndi madzi, ndi kulemba dzina lanu pa bukhu. Ndipo inu mumatenga dzanja lamanja la chiyanjano.”

79 Chabwino, Masonic Lodge ili ndi dongosolo labwinoko kuposa izo. Ndizo zowona. Masonic Lodge ndi malozi ena onse ali bwino, komabe iwo si nyumba ya Mulungu. Apo ndi pamene Mulungu amayankhula. Malozi amenewo amayesera kukupangani inu kukhala amakhalidwe abwino, koma Mulungu amakupangani inu olungama kudzera mwa Yesu Kristu, Mwana Wake. Tsopano, pali ndondomeko ya makhalidwe kwa izo; Mulungu ali ndi Kubadwa kwatsopano kwa inu.

80 Koma mveterani ku Liwu Lake laling’ono lodekha. Aliyense wa inu anthu amene mumadzinenera kuti ndinu Akhristu, dzikhazikeni nokha chete pamaso pa Iye. Musati mulole kuchapa kukulepheretseni. Musati mulole ntchito ikulepheretseni. Musati mulole chirichonse chikulepheretseni. Musati mulole aliyense adziwe zomwe inu mukuchita. Ingopitani pamaso pa Iye. Pitani mu nkhalango kwinkwaka. Pitani mmbali mwa msewu. Lowani mu chipinda chobisika ndi kutseka chitseko. Pamene ana apita kusukulu, pamenepo gwadani pamawondo anu. Inu mwamva maliwu amitundu yonse kulikonse, koma ingokhalani pansu ndi kukhala pamenepo mpaka maliwu amenewo atatontholetsedwa ndipo inu nkuyamba kukweza. Izo zidzakusinthani inu. Izo zidzakupangani inu mosiyana, monga Ilo linamuchitira Samueli wamng’ono uyu. Ilo lidzachita chinachake kwa inu ngati inu mutangochita izo. Tsopano, Ilo lidzakupangani inu chimene inu muyenera kukhala. Ilo lidzakupangani inu mtundu wa Mkhristu yemwe inu muyenera kukhala.

81 Tsopano tiyeni ife tibwerere mmbuyo ku tsiku lamakono ili, mpaka tsiku lomwe lapita. Tiyeni tibwerere ku masiku a nthawi yoyambirira. Ndipo Liwu ili la Mulungu lafika kwa anthu mu mbali zonse za moyo, mu mibadwo yonse. Ziribe kanthu ngati muli mlimi, ngati ndinu wosoka nsapato, chirichonse chimene inu mungakhale, Mulungu akuyankhulabe. Ngati ndinu wochimwa, ngati ndinu hule, hule, ngati ndinu chidakhwa, ngati inu muli (chiyani?) membala wa mpingo wamba, mwadzina—mwadzina, chirichonse chimene inu mungakhale muli, Liwu la Mulungu likudikirabe kuti liyankhule kwa inu.

⁸² Ine ndikuganiza tsopano za Mose, pamene iye anali kale zaka eyite, ndipo anali ndi zaka eyite za maphunziro a zamulungu. Ndipo iye ankawadziwa Malemba; iye ankawadziwa Iwo bwino. Ndipo iye anali nalo lonjezo kwa iye, kuti iye adzakhala wowombola wa anthu ake. Koma, komabe, kungodziwa Malemba ndi kukhala a—membala wa mpingo wokhazikika wa mpingo wamakono umenewo mu tsiku limenero, iye anachitengera chinthucho mmanja ake omwe ndipo anayesera kuchichita icho. Iye anapha m'Igupto. Inu mukuwona zomwe inu mumachita posamvetsera kwa Mulungu? Inu mumangozisokoneza izo.

⁸³ Ndipo pamene mdierekezi, mmawa uno, anganene, “Musati inu mubatizidwe.” Wina anganene, “O, muchite izo nthawi ina.” Wina anganene, “Inu kuli bwino mukhale wotsimikiza kuti inu mukudziwa zomwe mukuchita.” Ndipo winayo akuti, “Inu mudzataya nthawi yabwino.” Njira yokhayo yokhazikitsira zimenezo, ndi kupita ku Mawu a Mulungu ndi izo. Koma anthu, lero, sakuwoneka kuti akufuna kuchita zimenezo.

⁸⁴ Ndipo, Mose, iye anali atakhala kwa aphunzitsi opambana, koma iwo anafika pofunda ndi kuzizira. Iye anali atamva nkhani imene amayi ake anamuza iye, momwe kuti iye anabisidwa mu mantcheza, ndi momwe kuti ng'ona zikuluzikulu sizikanakhoza kumugwira iye. Momwe kuti, akuyandama chotsika pa mtsinje umenewo, anali mwana wamng'ono uja. Kumene a . . .

⁸⁵ Ng'ona zakalezo zinali zonenepa basi. (Izi ndi chifukwa cha ana aang'ono.) Izo zinali zonenepa, chifukwa cha kudya makanda aang'ono amenewo. Iwo anali nawo akazi akale a mphuno zangowi, apolisi aakazi, sanakhalepo ndi khanda, samadziwa momwe chikondi cha khanda chinaliri. Bwanji, iwo amangopita kunja uko ndi kukatenga ndi kupha ana aang'ono amenewo, ndi kuwaponyera iwo kunja mu mtsinje. Ng'ona zakale zimenezo zinali zonenepa basi, pa makanda amenewo.

⁸⁶ Ndipo, komabe, Mulungu anaika pa mtima wa mayiyo kuti ayike mwana wake mu imfa yomwe. Kodi inu simukuwona icho chinali choyimira cha Khristu? Iye anapita mpaka mu imfa. Ndipo iliyonse ya ng'ona zakale izo zinkakhoza kubwera ku basiketi laling'ono lija likupita chotsika ndi mtsinje. Inu mukudziwa chifukwa chake izo sizinakhoze kuchita izo, chifukwa chimene izo sizinakhoze kudya khanda limenero? Apo panali Mngelo atakhala pamenepo. “Chokani pano.”

⁸⁷ Chifukwa chiyani? Mulungu amawapatsa Angelo Ake ulamuliro kuti aziyang'anira anthu Ake. Musati muchite mantha, okonedwa. Mulungu akukuyang'anani inu. Mdierekezi akhoza kuyesera kuchita chinachake kwa inu, koma Mulungu ndi wamkulu. Mukuwona?

kotero, ng'onazo zimayenera kuthawa kuchoka ku basiketi yaing'onoyo.

⁸⁸ Ndipo, komabe, Mose ankadziwa zinthu zonse izi. Ndipo, komabe, zitatha zaka forte za kuphunzitsidwa, ndipo kenako mu chipululu, iye ankayeserabe kuti achitengere chinthucho, mmanja mwake.

⁸⁹ Ife timadziwa Baibulo, zimene Mulungu amanena kuti tichite, ndipo komabe ife timati, “Chabwino, tsopano, ife tipanga Izi kukhala mwanjira *iyi*. Ndizo, basi, masiku a zozizwitsa salinso choncho konse. Ife tikudziwa kuti sitikhulupirira kuti ife timaziwonanso, ndipo ife timakhulupirira kuti masiku a zozizwitsa anapita. Ndipo kukonkha ndi kwabwino basi ngati kumiza. Ndipo ‘Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera’ ndi zabwino basi monga Dzina la Ambuye Yesu. Ndipo kotero ife basi. . .Ena onse akupita mwanjira imeneyo, kotero ife tizingochita izo, nafenso.”

⁹⁰ Mose anali atakhala mwamuna wankhondo. Ndipo iye ankaganiza kuti njira imene iye anaphunzitsidwira, monga pokhala munthu wankhondo, kuti iye akanakhoza kungowapha Aigupto awo ndi dzanja lake. “Kungokhala wabwino basi monga kuchita zomwe Mulungu anachita.” Kodi inu munayamba mwaganizapo za izo? Aliyense amamutsutsa Mose chifukwa cha kupha munthu mmodzi. Ndipo iye anabwerera kumusi uko ndi kudzoza kwa Mzimu Woyera ndipo anapha chinthu chonsecho, palibe amene ananena kanthu za izo. Iye anapha ankhondo onse a Farao, koma Mulungu anali mu izo. Mulungu sanali mu woyambayo.

⁹¹ Ndipo kenako Mose, basi wodzaza ndi zamulungu za mpingo, iye anali woti adzakhale farao wotsatira. Ndipo ife tikumupeza iye, asakumudziwabe Mulungu.

⁹² Koma m'mawa wina, kuseri kwa chipululu, bambo wachikulire wa usinkhu wa zaka eyite, ndevu zake zikulendewera pansu, iye anawona chitsamba choyaka. Ndipo iye anapatuka kuti awone chimene chinali kuchitika. Ndipo pamene iye anafika pafupi ndi chitsambacho, iye anamva Liwu. Mulungu anayenera kumukhalitsa chete iye kwa zaka forte, iye asanakhoze konse kuyankhula kwa iye. Ndipo ife sitingakhala chete maminiti teni, kotero kuti Mulungu akhoze kuyankhula kwa ife, ndi phokoso lonse ndi zisokonezo zomwe ife tiri nazo za tsiku lino.

⁹³ Ndipo komabe, Mose, zitatha zaka forte, anayima pamenepo, ndipo mu Kukhalapo kwa chitsamba chimenecho. Ndipo Liwu limodzi lija lomwe linamuyitana iye, iye anadziwa zambiri za Mulungu mu maminiti faivi, zitatha izo, kuposa zomwe zaka zonse eyite zakuphunzira zinamuphunzitsa iye. Izo zinapanga munthu wosiyana kuchokera mwa iye.

⁹⁴ Izo zikupangani inu mwamuna ndi mkazi wosiyana kuchokera mwa inu, ngati inu mungoima njii motalika mokwanira kuti mumve Liwu Lake, monga Samueli anachitira.

Imani njii. Musati mukhale otengeka. Ngati inu mukufuna chinachake cha Mulungu, mufunseni Iye; ndiye imani njii ndi kumvetsera, muwone chimene Iye ati anene za izo. Ingotsegulani mtima wanu, nenani, “Nanga bwanji izo, Ambuye Yesu?” Ingokhalani pamenepo. Ngati Iye sayankha maora faivi oyamba, ndiye dikirani ena. Ngati Iye sayankha lero, ndiye Iye adzayankha mawa. Ngati Iye sayankha sabata ino, Iye adzatero sabata yamawa. Khalani pamenepo mpaka Iye atayankha.

⁹⁵ Imvani Liwu Lake likuyankhula mobwezera, mu mtima mwanu, ndi kuti, “Inde, Ndine Ambuye amene ndimakuchiritsa iwe.” Ndiye zonse zatha. Inu mukhoza kukhazikika ndiye. Mukuwona? “Ndine Ambuye Amene ndimakhululukira machimo ako onse. Tsopano pita ndipo usakachimwensho. Ine sindikukutsutsa iwe.” Ndiye inu mukhoza kupita mfulu. Inu muli bwino. Koma inu mumafuna kuti mukhale otsimikiza kuti inu munalimvadi Liwu limenero likuyankhula. Mose analimva Ilo. Iye anali munthu wosinthika.

⁹⁶ Tayang’anani pa Yesaya, mneneri. Monga mnyamata wamng’ono, iye anazipanga izo. Mfumu yaikulu yokonderedwa Uziya, mmasiku amenewo, munthu wolungama, munthu wabwino. Iye ankamukonda Yesaya, chifukwa iye ankadziwa kuti iye anali mneneri. Ndipo koteri iye anangotsamira pa mkono wa mfumu. Chirichonse chimene iye ankachifuna, bwanji, Uziya anachipereka icho kwa iye. Ndipo nthawi iliyonse iye akafuna chirichonse, bwanji, mfumu yabwino imapereka icho kwa iye. Koma inafika nthawi imene mfumuyo inafa.

⁹⁷ Kulemera kumawononga anthu nthawi zonse. Ndicho chinthu chovuta kuchinena. Koma kulemera kumamuchotsa munthu kwa Mulungu. Mulungu anayankhula malo amodzi, mu Baibulo, chinachake pa mzere uwu, ndipo Iye anati, “Pamene ine ndinakudalitsa iwe, ndi kukupatsa iwe zochulukana. Pamene iwe unali wosauka ndipo iwe unalibe kanthu, Ine ndinadza kwa iwe, ndipo iwe unandimva Ine ndipo iwe unanditumikira Ine. Koma pamene ine ndinakudalitsa iwe ndi kukupatsa iwe zochulukana, ndiye iwe unatembenezira mutu wako kuchoka kwa Ine.” Ndicho chimene Amereka yachita, anatembenzira mitu yawo.

⁹⁸ Ndicho chimene mipingo yachita. Inu mukhoza kukhala kunjira pa ngodya, ndi kukhala ndi nyumba zabwino zazikulu kwambiri, ndi mamiliyoni a madola pa . . . ataikidwa mmenemo, ndipo chirichonse chopheka basi monga icho chikanakhoza kukhalira. Nzosadabwitsa inu simunakhale nayo nthawi kuti mumvetsere Liwu la Mulungu. Koma dikirani mpaka ora lifike pamene izo zidzachotsedwa, ndiye inu mudzalakalaka kuti mulimve Ilo. Chirichonse chiri bwino tsopano, koma ora likubwera pamene izo sizidzakhala choncho.

⁹⁹ Chotero, Yesaya, iye ankakhoza kutsamira pa mkono

wa mfumu. Ndipo iye anali mnyamata wachichepere wokonderedwa, ndi mzimu wabwino mwa mnyamata uyu, kotero mfumu inkamukonda iye. Ndipo tsiku lina, zotsamira zinachotsedwa pansu pake. Mfumuyo inafa. Ndipo pamene mfumuyo inafa, ndiye Yesaya anayenera kuti azipita yekha. Ndipo kenako iye anayamba kuyang'ana pozungulira, ndipo iye anapeza kuti aliyense sanali monga mfumuyo.

¹⁰⁰ Inu mudzathamangitsidwira kunja, ena mwa masiku awa, kuchokera ku zipembedzo zosiyanasiyana izi monga ichi. Idzafika nthawi yomwe inu mudzayenera kukhala wa bungwe, kapena inu simungakhoze kupembedza. Monga inu mukudziwa, Lemba limati izo zidzakhala. Iwo amangokusekani inu tsopano. Koma padzakhala nthawi pamene padzakhale kunyanyala, pakuti chilemba cha chirombo chiyenera kudza. Inu mwina mudzakhala wa chitaganya cha mipingo, chirombo monga icho chiri mu Roma, kapena inu simudzapembedza konse. Ndizo zimene Lemba limanena. Ndi pamene inu mudzayenera kuti mudzalire monga Yesaya anachitira.

¹⁰¹ Ndipo iye anatsikira mu kachisi, ndipo iye anazindikira pamenepo. Iye anakweza manja ake ndipo iye anati, “O Ambuye, ine ndine munthu wa milomo yonyansa.” Inu mumaganiza kuti ndinu wabwino, koma dikirani mpaka nthawi imeneyo ifike. “Ine ndimakhala pakati pa anthu a milomo yonyansa.” Kodi iye anachita chiyani? Anafika posimidwa.

¹⁰² Ndipo pamene inu mufika posimidwa za chinthu ichi, chinachake chichitika. Inu simuli wosimidwa mokwanira. “O, chabwino, ine ndinajowina mpingo. Izo zikukhazikitsa izo.” Koma inu mukuyenera kukhala wosimidwa za izo. Inu muyenera kumusowa kwenikweni Mulungu.

¹⁰³ Yesu anati, “Odala ali iwo akumva njala ndi ludzu la chilungamo, pakuti iwo adzadzazidwa.”

¹⁰⁴ Koma malingana ngati inu muli wokhutitsidwa ndi zinthu za mdziko, kodi Mulungu angakhoze bwanji kuyankhula kwa inu? Inu mumati, “Mulungu sanayankhule kwa ine.” Bwanji? Iye akufuna kutero. Koma inu muli odzazidwa kwambiri ndi zinthu za mdziko. Ndilo lomwe liri vuto ndi ife lero. Ife timayika nthawi yathu yonse pa zinthu za mdziko, ndi zosangalatsa za mdziko, ndipo osapereka nthawi kwa Mulungu. Ndizo zowona.

¹⁰⁵ Tsopano, ife tikupeza kuti Yesaya anafika posimidwa. Ndipo iye anafuula mokweza, ndi kuvomereza machimo ake, ndi kuvomereza machimo a anthu. Pamene iye anamaliza kuvomereza, iye anamva phokoso pamwamba pake. Ndipo pamene iye anayang'ana mmwamba, apo panali Akerubi, akuwulukira mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa mnyumbamo. Mapiko pamwamba pa nkhope Zawo, ndi mapiko pamwamba pa mapazi Awo, ndi kuwuluka ndi mapiko, akufuula, “Woyera, woyera, woyera, Ambuye Mulungu Wamphamvuzonse.”

¹⁰⁶ Chinachake chinali kuchitika. Yesaya anafika posimidwa. Mulungu anabwera pa ntchito. Ndipo Yesaya anafuula, “Ine ndiri ndi milomo yonyansa,” pakuti Liwu linali litangoyankhula kumene. Ilo linamusintha iye.

¹⁰⁷ “Ndani ati atipitire Ife?” linatero Liwulo. “Ndani ati apite? Ndani ali wololera kuyima pakati, pakati pa gulu ili la azamulungu? Ndani ati apite mu tsiku lino, ndi kukalengeza kuti Ine ndikadali Mulungu? Ndani ati apite ndi kukatsutsa kusayera kwawo? Ndani ati akaphwasule zipembedzo zawo ndi kukamanganso mphanvu za Mulungu wamoyo kachiwiri? Ndani ati apite?”

¹⁰⁸ Yesaya anati, “Ambuye, ine ndisanakhoze kupita, ine ndiyenera kusinthidwa.” Ena mwa mantha aang’ono awa ndi zokhumudwitsa zinkayenera kumusiya iye.

¹⁰⁹ Momwemonso zidzakhala ndi munthu aliyense amene Mulungu adzamuyitana! Inu muyenera kukhala wobadwanso kachiwiri, wosinthidwa ndi kupangidwa mwatsopano. Osati kulingalira; koma kuchokera mu mtima mwanu, chinachake chimene chimachitikadi. Ndipo mmodzi mwa Angelo... “Ngati inu mupempha, inu mudzalandira.”

¹¹⁰ Mmodzi mwa Angelo anapita ku guwa la mkuwa, ndipo anatenga zopanira nafikira ndipo anatenga khala la Moto wamoyo, ndipo anathamangira kwa Yesaya naliika ilo mkamwa mwake. Anati, “Tsopano wayeretsedwa. Pita, ukayankhule Mawu.” Yesaya anasinthidwa atatha kumva Liwu limenero.

¹¹¹ Ndiyeno kumapeto kwa zaka zake, iye analemba Baibulo lathunthu. Iye anayambira pa Genesis ndipo anatsirizira mu Chivumbulutso. Pali Mabuku sikisite sikisi a Baibulo; pali mitu sikisite sikisi a Yesaya. Chifukwa chiyani? Chifukwa iye anafika posimidwa, mu nthawi yomwe iye anawona Iko kukusowekera kwambiri.

¹¹² Danieli, mu Babeloni, monga ife tinayankhula za iye usiku watha. Iye anali atatsimikiza mumtima mwake kuti iye sadzadzidetsa yekha ndi ziphunzitso za Babulo. Koma tsiku lina, kumusi uko, Danieli anafika mu kusowa. Ndipo iye anakadziwa kuti iye ankafuna kumva Liwu la Mulungu, komabe iye anali nawo Malemba. Koma iye ankasowekera kuti amve Liwu la Mulungu. Ndipo iye anapita ku mtsinje *wotero*. Ndipo iye sanangopita kumeneko ndi kuyimitsa galeta lake ndi kugwada pansu mu mantcheza, ndi kunena, “Ambuye Mulungu, ine ndikufuna kuti ndikumveni Inu. Inu muli kuti?” Ayi. Inu simumachita izo mwanjira imeneyo. Yesaya anali atatenga galeta lake, ndi oyendetsa, ndipo anali atapita ku mtsinje ndi kuwabweza iwo. Iye anali woti akhale mpaka iye atamva. Ndiyo njirayo. Iye anafika posimidwa za izo.

¹¹³ Iye an kayenera kuti apite kutali kwambiri ndi asirikali onse, ndi akasidi onse, ndi amuna anzeru, madokotala onse

a zamulungu, ndi ena otero, amene anali kuyesera kumuwuza iye, “Izi! Iwe uchite *izi*, Danieli. Iwe uchite *izi*, Danieli.” Koma iye anachoka ku zonse za izo. Umo ndi momwe inu muyenera kuchitira. Ndipo iye anatsikira pa mtsinje, ndipo iye anakhala kumeneko kwa masiku twente wani, akulimbana ndi Mngelo wa Ambuye.

114 Koma ife timauzidwa kuti iye anayang’ana pa madzi. Pamenepo iye anawona Mngelo atayima, ndi phazi Lake pa mtunda ndi pa nyanja. Ndipo anakweza mmwamba manja Ake nalumbira pa Iye amene ali moyo kwanthawi za nthawi, “Pamene zinthu zimene Danieli anaziwona zidzachitika, nthawi sikuyenera kukhalaponso.” Iye anachedwetsedwa masiku twente wani chifukwa cha zoipa za mdziko.

115 Ndipo ngati Iye anachedwetsedwa masiku twente wani chifukwa cha zoipa za mdziko limenero, mmasiku a Peresiya, kodi Iye akanakhala chiyani mu tsiku ili? Kodi Iye akanakhoza kuchedwetsedwa motalika bwanji? Koma chikhulupiriro chosafa chimenecho, njala imeneyo ndi chikhumbo mu mtima wa munthu, zomwe sizinganene ayi kwa Mulungu, koma zigwiritsitsabe mpaka Mulungu atayankhula kuchokera Kumwamba. Inu simungakhoze kusewera ndi uwu, ndi Uthenga uwu. Iwo si woti uziseweretsedwa. Iwo uyenera kugunda pa nsomali, teni pa teni. Iwo uyenera kukhala wangwiro, kapena izo sizolondola ndipo sizigwira ntchito. Iwo uyenera kukhala wangwiro. Danieli anapemphera.

116 Ife tikupeza mu Baibulo, cha pafupifupi mutu wa 8, mutu wa 7 kapena wa 8 wa Bukhu la Machitidwe, kuti, wamng’ono, Mfarisi wamng’ono wodzipanga yekha dzina lake Saulo. O, iye anali wazamulungu, chabwino. Iye anali atakhala pansu pa chiphunzitsa cha Gamaliyeli ndipo iye anali nawo Malemba onse, pansu pomwe mwa njira yomwe izo ziyenera kukhalira, molingana ndi azamulungu a tsiku limenero, o, odzikonza okha ndi odzipanga okha. Ndipo iye anawawona anthu akuchita chinachake chimene chinali chauzimu, ndipo fiyoloje yake yopangidwa ndi anthu siinagwirizane nazo Izo.

117 Ndi kufanana kotani nanga kwa lero! Woono ndi woonamtima mu mtima mwake, monga anthu ambiri aliri, iwo amaganiza kuti anthu amene anabadwa mwatsopano ndi openga. Iwo amaganiza kuti machiritso Auzimu ndi mphamvu za Mzimu Woyera ndi chinachake chimene iwo *amachikamba*, koma izo nzooona.

118 Koteru pamene iye anali pa ulendo wake wopita ku Damasiko, tsiku lina, ndi malamulo ena mthumba mwake, kuchokera kwa—kuchokera kwa bishopu wa mpingo, kuti apite kumusi ndi kukawononga gulu lonse lija la oyera odzigudubuza amene anali kukuwa ndi kufuula, ndi—ndi kudumphamba mmwamba ndi pansu, ndi kuyankhula ndi zinenero

zachilendo, ndi—ndi kuchiritsa odwala. “Ndipo, bwanji, ndi gulu la ziwanda,” anatero azamulunguwo. “Pita uko ndi kukawamanga iwo, ndi kuwabweretsa iwo kuno ali mu unyolo!”

¹¹⁹ “Ndithudi. Pa ntchito yanu, bishopu!” O, mai! O, iye anali munthu wamkulu. Iye anali ndi D.D., Ph. D., inu mukudziwa. Chotero iye anali atalumphira pa kavalo wake, ndipo kutali iye anapita, ndi gulu pamodzi ndi iye.

¹²⁰ Koma panjira yake, pafupifupi masana, Chinachake chinamugwetsa iye pansi. Ndipo iye anagudubuzika mu fumbi, ngati munthu wamisala, akutulutsa thovu. Ndipo iye anamva Liwu likuti, “Saulo, Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?” Chinali chiyani icho? Osati ena a zamu-...zamu-... wazamulungu akuyankhula kwa iye. Koma Liwu lochokera Kumwamba, “Chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

¹²¹ Ndipo iye anatembenuzika mu fumbi, ndipo makwinya ake onse odzaza ndi fumbi, ndi misonzi ikutsikira mmasaya ake, mwinamwake. Iye anati, “Ambuye, Ndinu Yani?” Ndipo pamene iye anatsegula maso ake, iye anakhala wakhungu ngati mleme.

¹²² Apo panayima Lawi la Moto lalikulu patsogolo pake. Ndipo Liwu likuchokera kwa Ilo, linati, “Ndine Yesu, Amene iwe ukumuzunza. Chiphunzitso chako chopangidwa ndi anthu chakhala chiri cholakwika.” Chinali chiyani icho? Apo panali masomphenya otseguka. Mawu a Mulungu anapangidwa kukhala enieni.

¹²³ O, abale, ndicho chimene ife tikusowa lero, ndi zina zochulukana monga zimenezo.

¹²⁴ Ine ndikungofuna kumuthokoza Ambuye. Atsikana aang’ono awa, ali mu zikuku usiku watha, akubwera, akuyenda lero, ndipo opanda zikuku, kotero iwo akupita. U-nhu. Ambuye akudalitseni inu, atsikana, mwakhala pamenepo. Nchiyani chinachita izo? Yesu yemweyo amene anayankhula mu Liwu lauzimu kumbuyo uko, akuyankhulabe lero.

¹²⁵ “Saulo, Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?” Saulo anali munthu wosinthika.

¹²⁶ Ndipo anthu akuyenera kusinthidwa lero pamene iwo angakhoze kuwona ndi kumva Liwu la Mulungu wamoyo likuyankhula monga Iye anachitira pamene Iye ankayenda mu Galileya. O, ndithudi!

¹²⁷ “Saulo, Saulo, chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?” Nchiyani chinachita izo? Kodi Iye anamutengera iye ku seminare ndi kukamuphunzitsa iye zamulungu zina zatsopano? Ayi, Iye sanatero. Kodi Iye anachita chiyani? Iye anayankhula kwa iye, ndipo apo panali Liwu lenileni likuyankhula kudzera mu Mtambo. Chinali chiyani icho? Mulungu yemweyo amene anabingula kuchokera pa Phiri la Sinai.

¹²⁸ Mmisonkhano, mmalo omwe Mzimu Woyera umabwera, inu mumamva liwu la munthu likusinthika. Ndipo osadziwa nkomwe, ma ABC, koma Khristu akhoza kutenga liwu limenero ndi kuyankhula zinsinsi za Mulungu Wamphamvuzonse. Izo ziyenera kumusantha mwamuna ndi mkazi aliyense yemwe akukhala mu Kukhalapo Kwake...?..."Ine ndinamva Liwu," iye anatero. O, ife tikugona kwambiri. Ine ndikuyembekeza izo sizitero, sizidzayenera kupangidwa momveka bwino kuposa pamene. Koma ife timagona kwambiri m'mipingo yathu, mu zamulungu zathu, mu kuganiza kwathu, ndi mu njira zathu zamoyo, mpaka ife timalephera kulimva Liwu limenero pamene Ilo likuyankhula.

¹²⁹ "O," iwo amati, "izo zikhoza kukhala zam'webwe. Izo zikhoza, inu mukudziwa, zikhoza kukhala *izi, izo*, kapena *zinazo*."

¹³⁰ Bwanji ngati Mose akananena, "Kuti, ndikudabwa ngati icho chinali chiwanda mu chitsamba chija?" Huh! Panalibe funso kwa Mose, iye analimva Liwulo.

¹³¹ Ngati inu mukuti, "O, icho chikhoza kukhala chikumbumtima changa chikundiwa ine zimenezo."

¹³² Ngati inu muli mwana wa Mulungu, inu mudzadziwa kuti ndi Liwu Lake. "Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa. Nkhosa Zanga zimamva Liwu Langa." Iwo adzadziwa.

¹³³ Panali wina, dzina lake Petro, amene anakhala wopulumutsidwa, ndipo analinso wodzadziwa ndi Mzimu. Ndipo iye ankafunabe kukangamira miyambo ya akulu. Zonse zomwe iye akanadziwa, zikanakhala ziri umu mu Mawu. Ndipo tsiku lina, ali padenga la nyumba, pamene iye ankafuna kusunga miyambo ya, "Musadye nyama...kudya nyama iliyonse, ndi masabata, ndi zina zotero." Pali anthu ambiri abwino omwe amayeserabe kukangamira pa zinthu monga zimenezo.

¹³⁴ Ndipo tsiku lina pamene iye anali pamwamba pa denga la nyumba, iye anamva Liwu limene linati, "Usati uzitche zomwe Ine ndaziyeretsa, 'zodetsedwa.'"

¹³⁵ Mulungu, ine ndikukhumba Iye akanatenga gulu la alaliki mu chigwa ichi kuno, ndi kuwalola iwo adziwe kuti ife sitiri openga, ife sitiri oyera odzigudubuza, mulu wa zinyalala. Ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo. Ndipo amuna ndi akazi aledzera ndi ubwino Wake. Si ufiti kapena kuwerenga maganizo. Ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo. Tayani miyambo yanu, akulu, ndipo mvetserani ku Liwu la Mulungu wamoyo. Ilo lidzakusinthani inu. Inu simudzakhala mmodzi wa ozunzawo. Inu mudzafuna kuti mukhale mmodzi wa iwo. Ngati inu mungakhoze kudutsa zotchinga za ziphunzitsa zanu zonse, mpaka inu mutakhoza kuyandama mu Kukhalapo Kwake kutsidyako, chinachake chidzachitika. Inu simungakhulupirire kuti masiku a zozizwitsa apita. Inu mukhulupirira kuti iwo

ali pomwe pano, chifukwa chimodzi chichitidwa pa inu, zedi, kuti chimusinthe munthu. Ndicho chimene Liwu la Mulungu limachita nthawizonse. Ilo limawasintha amuna ndi akazi ndi kuwapanga iwo chimene iwo ayenera kukhala; osati zomwe masukulu ndi aphunzitsi apanga, koma zomwe Mulungu wawapangira iwo.

Liwu, likuyankhula! “Ine ndinamva Liwu.”

¹³⁶ O, momwe ine ndikanafunira kuti ndilowe mu zondichitikira zanga. Ndipo momwe inu mungakondere kupita ku maumboni aumwini, ambiri a inu amuna ndi akazi amene mwamva Liwu Lake.

¹³⁷ Ndipo ine ndikukhoza kukumbukira za kulimva Ilo pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono chabe, kutali komwe m’mapiri a ku Kentucky. Ndipo ine ndinaganiza Iyo inali mbalame itakhala mu mtengo, koma mbalameyo inawulukira kutali. Iye anati, “Usati uwope, chifukwa iwe udzachoka kuno tsiku lina, ndi kukakhala pafupi ndi mzinda wotchedwa New Albany.” Ine ndinamva Liwu Lake pamene Iye anati, “Usati usute, kapena kumwa, kapena kuipitsa thupi lako ndi akazi ndi zina zotero. Pali ntchito yoti iwe udzachite pamene iwe udzakula.”

¹³⁸ O, Iye akadali Ambuye Mulungu yemweyo. Ndipo inu mumamumva Iye, ora ndi ora, akuyankhula kwa inu mu chipinda chanu chaching’ono, mu chipinda chanu chopempherera. Akutuluka pamaso pa omvetsera, ndiye nkuyankhula mowonekera kwa anthu. Liwu la Mulungu, Ilo linali lamtengo wapatali mmasiku a Samueli. Ilo ndi lamtengo wapatali kwambiri lero. Pakuti, panalibe masomphenya otseguka.

¹³⁹ Petro analimva Liwulo, ndipo Ilo lina sintha za fiyoloje zake zonse. Iye anapita molunjika kumene kwa Amitundu, amene iye ankaganiza kuti anali gulu la anthu osaphunzira otayidwa. Koma, Liwu la Mulungu, osati kuphunzitsa kwake, Liwu la Mulungu wamoyo linamusintha iye.

¹⁴⁰ Ndipo tsopano mmodzi yekha. Panali mwamuna wabwino, nthawi ina, mu Baibulo. Wodziwana naye Yesu, amene anamkonda Iye, ndipo anakhulupirira mwa Iye, ndi kumpembedza Iye, ndi kusewera ndi Iye, ndipo anapita mmapiri ndi Iye, natsikira ku mtsinje, akuwedza ndi Iye. Iye anali munthu wabwino. Tsiku lina, pamene Yesu anali atachoka, imfa inadza kudzaba mu chipinda chake.

¹⁴¹ Ndipo iye anali atasiya mpingo wakale wa orthodox, iye ndi alongo ake okondeka, Marita ndi Maria. Ndipo iwo anali atatuluka chifukwa iwo ankamukonda Iye, ndipo ankamukhulupirira Iye kuti anali Mesiya. Ndipo pochita zimenezo, mpingowo unawachotsa iwo mwamsanga.

¹⁴² Ndipo mnyamata uyu anadwala kwambiri mpaka iye anafa, ndipo anali atayikidwa m’manda, masiku foro. Kodi ziphunzitsa

zamulungu zikanachita ubwino wanji pamenepo? Ndi ubwino wanji kwa mpingo wake ndiye? Koma apo panali Liwu la Mulungu, pa dziko lapansi, ndipo Iye anayankhula kwa Lazaro. Ndipo Lazaro, mwamuna yemwe anali wakufa ndi wovunda mmanda, anamva Liwu Lake, ndipo anatuluka nakhalanso moyo kachiwiri.

¹⁴³ Ine ndinali wakufa kamodzi, mu uchimo ndi zolakwa. Inu munali akufa mu uchimo ndi zolakwa. Koma linali Liwu la Mulungu limene linati, “Idzani kwa Ine, inu nonse olema ndi othodwa, Ine ndidzakupatsani inu mpumulo.”

¹⁴⁴ Ine ndawonapo Liwu likuyankhula kwa wolumala, kumuwongola iye. Ine ndinawona Liwu la Mulungu likuyankhula kwa wakhungu, ndipo maso ake anatseguka. Kwa akufa, ogwidwa ndi khansara, kwa wakhate, kuwawona iwo akubwerera mu mnofu, mu thanzi langwiwo kachiwiri. Ine ndamuwona Iye akuyankhula kwa zidakwa, ndi ozunguzika ubongo, ndi otayidwa, ndi gulu la osauka, ndipo iwo akukhala madona ndi njonda, ndi overa a Mulungu wamoyo, chifukwa Liwu la Mulungu linayankhula. Ndi zomwe ife timamvera, lero.

¹⁴⁵ Ndiloleni ine nditseke pakunena izi. Idzafika nthawi, kuti pamene solo yanu yoyendayenda idzachotsedwa mu thupi lanu, ndipo iyo ili mu kopita kwake kwinakwake, kuyendayenda kutsidya mu mdima, kapena mwina mu zifuwa za Mulungu. Liwu limenero lidzayankhulanso kachiwiri. Ndipo Baibulo linanena, kuti, “Onse amene ali mmanda adzamva Liwu Lake, ndipo adzatuluka kunjja. Ena adzafika ku manyazi ndi mnyozo wosatha; Ndipo ena adzatulukira ku mtendere ndi chimwemwe chosatha.”

¹⁴⁶ M'mawa uno ukhoza kukhala nthawi yoti inu mupange lingaliro lanu, kaya inu mumvetsera ku zimene televizioni ikunena, kapena zomwe pepala likunena, kapena zomwe azamulungu akunena, kapena zomwe Mulungu akunena. Ndiloleni ine ndikuuzeni inu, monga anthu. Inu musati muzimvetsera ku zimene chirichonse chikunena, koma chimene Mulungu akunena. Dikirani pa Liwu lodekha, laling'ono ilo, ndipo Iye adzakusinthani inu.

¹⁴⁷ Inu mukuti, “Ine ndingakonde nditakhulupirira, M'bale Branham. Ine ndikanakonda ndikanakhulupirira. Ine ndikanakonda ndikanachita zinthu zinazake.” Koma inu simungathe. Chifukwa chiyani? Inu simumakhala chete motalika mokwanira. Inu simumafika pamalo pomwe ku—kukayikira konse kwachoka.

¹⁴⁸ Pamene inu mulowa m'malo amene kukaikira kwapita, ndiye inu mudzakhala mfulu, ndipo inu mukhoza kumva Liwu la Mulungu likuyankhula. “Mwana Wanga, Ine ndine Mpulumutsi wako. Mwana Wanga, Ine ndine mchiritsi wako. Iwe sukuyenera kumachita zinthu izi. Ine ndinafa kuti iwe ukhale mfulu. Koma

pokhapokha ngati inu muli pansi apa mu kugwedezeka uku, kusakanizikana ndi mitundu yonse ya maliwu, ingozungulira kutali kuchoka kwa onse a iwo.”

¹⁴⁹ Zimandikumbutsa ine nthawi ina yomwe ine ndinali kumapiri kamodzi. Ndipo ine sindidzaiwala zondichitikira izo. Ndipo kuno pafupifupi zaka teni zapitazo, kapena osati motalika kwambiri, ine ndinali kuwathandiza Bambo Jefferies pa kusonkhanitsa, ndipo pamene iwo anali kukhala ndi mchere pa akavalo. Ndipo ine ndinali kuwatengera iwo ku malawi ena kumene ine ndikanakhoza kuwaika iwo, kumene ng’ombe zikanadziwa kuti zibwere. Kumbuyo komwe, mailosi sevente, pafupifupi, kuchokera ku chitukuko. Kapena, ine ndikutanthauza, pafupifupi mailosi sarte, sarte-faivi, mwinamwake mailosi forte, kupita ku Kremmling, Colorado, komwe inu mumafika mu mzinda wawung’ono wokhala ndi anthu pafupifupi seveni kapena eyiti handiredi. Ndipo ine ndinali ndi kavalo wanga, ndipo ine ndinatulutsa zikwama kunja, ndinazitsitsa. Ndipo ife tinayang’ana pa... kusaka ng’ombe kudzera mu zoyang’anira. Ndipo ine ndinali nditakoletsa kavalo wanga ku nthambi, ndipo ngolo zinali kumbuyo kwa iye, yemwe ali, kavalo...kavalo wa belu ali kutsogolo. Ndipo ine ndinapita pamwamba pa mapiri. Ndipo iko kunali kokongola kwambiri. Iyo inali nthawi ya kuphukira. Ndipo ine ndinali kuyang’ana kudutsa zigwa, ndikuyang’ana mafunde aang’ono a madzi, mmbuyo chapatali. Ndipo pamene ine ndinayang’ana, iwo unali pakati pa masana, ndipo ine ndinawona chinachake chimene chinandikondoweza ine.

¹⁵⁰ Ine ndinawona mayi wachikulire akutenga ana ake kuchokera mu chisa chake, mbalame yokalamba ya mphungu. Ndipo iye anawulukira mozungulira pa iwo mpaka iye anawatengera iwo pa mapiko ake. Ndipo iwo anali atatuluka kale mu chisa. Koma iye anawatengera iwo mu chigwa. Iwo anali asanafikeko kumeneko kale. Iwo amangophunzira kuwuluka. Chotero, iye anawasiya iwo. Ndipo iwo anapita motsatira, akutola udzu, ndi kugwera pa wina ndi mzake, basi mosasamala momwe iwo akanakhoza kukhalira. Ndipo ndiri chikhulire pamenepo, ine ndinaganiza, “Tsopano, kodi izo siziri monga gulu la enieni, Akhristu okhulupirira! Iwo ndi osasamala.” Chifukwa chiyani iwo anali osasamala? Iwo sankayenera kuti aziwopa chirichonse, chifukwa amayi anali atabwerera mmwamba ndi kukakhala pansu pa thanthwe, kuti awayang’anire iwo. O! Izo zimangosinthwa izo mochuluka.

¹⁵¹ Pamene inu mufika ku kuganiza, “Kodi Abusa *Akuti-ndi-akuti* aganiza chiyani ngati ine nditalandira Mzimu Woyera? Kodi Bishopu *Wakuti-ndi-wakuti* anena chiyani?” Ine sindikusamala zomwe iwo akunena.

¹⁵² Yesu anafa, ndipo Iye anakwera makonde a Ulemerero, ndipo Iye akukhala mmiyamba ya kumwamba. Palibe chimene

chidzakuvutitseni inu. Diso lake liri pa mpheta, ndipo ine ndikudziwa kuti Iye amandiyang'anira ine, ndipo Iye amakuyang'anirani inu.

¹⁵³ Ndiye pamene apo pabwera, ngati apo pangabwere nkhandwe, kapena chinachake choti chisokoneze mmodzi wa aang'ono awa, bwanji, iye. . . Iwo akanakhala bwino asatero. Iye amakhoza kunyamula nkhandwe mu dzanja lake, mu zikhadabo zake, kumunyamula iye mmwamba pafupifupi mapazi masauzande angapo ndi kungomusiya iye. Iye angathe kusweka m'mlengalenga. Palibe chimene chiti chiwavititse aang'ono awo. Iye aziwonetsetsa izo.

¹⁵⁴ Palibe chimene chiti chidzakuvutitseni inu. Musati muwope kumutenga Mulungu pa Mawu Ake. Ingomasukani, ndi kukhala ndi chikhulupiriro, ndi kukhulupirira. Iye akukuyang'anirani inu. Iye adzaphwasula chirichonse chomwe chingayesere kukuvutitsani inu. O, icho chikhoza kukuukirani inu, koma icho sichingathe kukuvulazani inu. "Pakuti zinthu zonse," Iye amazilola izo. Icho sichingakhoze kukhala chinanso, "Pakuti izo zikugwira ntchito limodzi kwa ubwino, kwa iwo amene amakonda Ambuye." Palibe chiopsyezo chingabwere kwa inu.

¹⁵⁵ Ndipo kotero, patapita kanthawi, apo panadza mkuntho. Ndipo pamene mkuntho unayamba, iwo umabwera mofulumira, yakumpoto iyo, kung'anima pang'ono kwa mphezi ndi mphero iyo ikubwera, mailosi sikisite kapena sevente pa ora. Ndipo mayi mphungu wachikulireyo anafuula mokweza kwambiri, ndipo pansu kudutsa chigwacho iye anapita. Ndipo kufuula uko, kodi iko kunachita chiyani? Mphungu zazing'ono izo zinkadziwa liwu la mayi wawo.

"Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa," Iye anatero.

¹⁵⁶ Choopsya chinali pafupi. Tsopano, iwo sanayesere kuti akhale pansu pa tizidutswa. Iwo sanayesere kuthamangira ku mtundu wina wa mulu wa zinyalala. Iwo anangowadikirira amayi.

¹⁵⁷ Ndicho chimene Mkhristu ayenera kuchita; onani zomwe Mulungu ati achite pa izo.

¹⁵⁸ Ndipo pamene ma—mayi wachikulireyo anatera pansu, mapazi akuluakulu awo pafupifupi monga *choncho*, iye anangoyenda pansu ngati ndege yaikulu ikutsika pansu. Ndipo iye anaponyera mutu wake mlengalenga nafuula, ndipo iye anaponyera mapiko aakulu awo kunjira, pafupifupi mapazi fortini, kuchokera kunsonga kufikira kunsonga, kutambalala monga kuchokera ku mtengo *uwu* kufika ku *uwo*. Mphungu zonse zazing'ono izo zimangothamanga molimba momwe izo zikanakhoza, ndipo zinalumphira pa mapiko a mayi wawo. Zinafikira pansu ndikugwira ndi timapazi tawo tating'ono, anatenga milomo yawo yaying'ono, ndipo anagwira imodzi ya nthenga zolimba izo mmenemo. Amayi

anangowatenga iwo, popanda kugwedezeke kwa mapiko awo, ndipo anakwera mmwamba mu mphepo imeneyo. Molunjika kumene mmathanthwe iye anapita, kuti akawabise iwo ku mkuntho umene unali kubwera.

¹⁵⁹ O, m'bale, mkuntho wayandikira pafupi. Imvani Liwu Lake. Ilo likuyitana kwa inu, "Tulukani mu Babulo. Khalani olekanitsidwa. Musakhale ogawana naye, machimo awo. Ine ndidzakulandirani inu. Inu mudzakhala ana aamuna ndi aakazi kwa Ine. Ine ndidzakhala Mulungu kwa inu."

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi yokha, mu kutseka. [M'bale akupereka ulosi—Mkonzi.]

¹⁶⁰ Amen. Inu munamva izo. Ndicho chimene ife timachitcha ulosi mu mpingo.

¹⁶¹ Kodi pangakhale ena pano mmawa uno, amene ine ndikudziwa alipo, amene angati anene, "Ambuye Mulungu, khalani wachifundo kwa ine. Ngakhale ine ndajowina mpingo, ine ndapanga kuvomereza, koma ine—ine sindikudziwa chomwe icho chiri kuti ndikhale chete pamaso Panu, ndi kumva Liwu Lanu likunditsogolera ine ndi kundiphunzitsa ine. Ine sindingadziwe choti ndichite ngati Inu mungayankhule kwa ine mu Liwu lomveka. Ine ndikanakonda kuti ndikudziweni Inu, kuti Inu mukakhoze kuyankhula kwa ine ndi kulondolera njira zanga"? Kodi inu mungakweze manja anu pakali pano ndi kunena, "Mulungu, khalani wachifundo"? Ambuye akudalitseni inu, kulikonse, manja kulikonse. Ingopitirirani kuwakweza iwo mmwamba. Uko nkulondola. "Ambuye, khalani wachifundo kwa ine. Ine ndikukusowani Inu kwambiri." Kodi pangakhale enanso basi tisanatseke? Mulungu akuwona manja anu kumbuyo uko, dona, ndi inu nonse mmbuyomo, ndi oyimirira mmizere ndi ena otero. Mulungu akukuwonani inu, ngakhale ku nsanja, pamwamba mozungulira kuno.

Ndipo Samueli anati, "Eli, kodi inu munandiitana ine?"

Eli anati, "Ayi, mwana wanga, ine sindinakuitane iwe."

¹⁶² Ameneyo sanali ine amene ndinayankhula kwa mtima wako, mzanga. Ameneyo anali Mulungu. Ingoyankhani mobwezera ndi kunena, "Wantchito wanu akumva. Ndipo nditengereni ine mu chisamaliro Chanu, lero, Mulungu. Ndiloleni ine, kuyambira lero, ndikhale Wanu kwathunthu."

¹⁶³ Mulungu wamuyaya, wokonda wa moyo, Mlengi wa zinthu zonse, pamene Liwu laling'ono lodekha lija la Mulungu limene linayankhula kwa Samueli, limene linayankhula kwa Saulo, limene linayankhula kwa Petro, limene linayankhula kwa Danieli, ndi Yesaya mneneri, ndi onse kupyola mmibadwo, layankhulanso kachiwiri mmawa uno mu kachisi. Mwinamwake mwina sarte, kapena forte, kapena mwina manja fifite, a ochimwa ndi mamembala a mpingo, ndi anthu okhala ndi zokhumudwitsa, anakweza manja awo. Ambiri a iwo anali pano

usiku watha, ndipo iwo anamva Liwu Lanu likubwera momveka. Ndipo tsopano, mmawa uno, Liwu lomwelo likuyankhula pansi mozama mu mtima mwawo. Iwo akweza manja awo, ndi manja awo kuloza Kumwamba, akunena kuti iwo ndi olakwa, ndipo iwo akufuna kuti akhale olondola.

¹⁶⁴ Inu mwanena m'Mawu Anu, kuti, "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba. Ndipo onse amene ati adzabwere, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya. Ndipo ndidzamuukitsa iye pa tsiku lomaliza."

¹⁶⁵ Inu munalonjeza izo, Atate. Tsopano ife tikuyitanira pa Inu, monga wantchito Wanu, kuti mupereke kwa awa omwe akweza manja awo, Moyo Wamuyaya ndi chimwemwe Chamuyaya. Ndipo mulole iwo akukhalireni Inu moyo, masiku onse a moyo wawo. Ndipo kumapeto kwa msewu wa ulendo wa moyo, kulowa mu chimwemwe cha Ambuye. Perekani izi, Atate. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu ndi chifukwa cha Yesu. Amen.

¹⁶⁶ Ndi angati a inu mukumukonda Iye ndi mtima wanu wonse, basi mtima wanu wonse? Tsopano, mmalo aang'ono awa apa monga chonchi. . . Ine ndachedwa basi. Koma Baibulo linanena, kuti, "Ife tikukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu." Mzimu Woyera umabwera, umalowa m'Mawu, umatsika pansi kudutsa mwa omvera, ndipo inu mukhoza kungowuyang'ana Iwo pamene Iwo ukusesa pa iwo, ukuwasinthwa iwo.

¹⁶⁷ Monga ine ndanenera, ine ndimakhulupirira mu zomverera. Zedi. Koma, inu, chiyani. . . Mwawona, zomverera sizimakusinthani inu. Zomverera zimayenera kulowa mkati mpaka kudzakhudza makhalidwe a umunthu wanu. Ndicho chimene chimakusinthani inu kuchoka ku wauchimo. . .

¹⁶⁸ Kodi wochimwa ndi chiyani? Wosakhulupirira. Pali anthu ambiri lero, ali ndi a—digirii ya Bachelor of Art, ndi digiri ya udokotala, ndi Ph. D., ndi ma L. D. awiri pa dzina lawo, ndipo akadali ochimwa. Amadziwa Baibulo kuchokera ku Genesis mpaka Chivumbulutso, amalalikirira pa guwa, ndipo komabe okhulu- . . . osakhulupirira. Baibulo linati, "Iye amene sakhulupirira watsutsidwa kale."

¹⁶⁹ Kumufunsa mmodzi wa anthu amenewo ngati amakhulupirira kuti Mzimu Woyera uli wa lero. "Bwanji, ayi ndithu." Kodi inu mukukhulupirira kuti machiritso Auzimu ali? "Bwanji, ayi ndithu." Ndiye iye ndi wosakhulupirira. Uko nkulondola. Ngati Mzimu Woyera uli mwa inu, kodi Iye sadzachitira umboni kwa Mawu Ake Omwe? Ndipo ngati mzimu uli mwa inu uchitira umboni mosiyana ndi zomwe Mulungu akunena kuti nzoona, si Mzimu wa Khristu. Inu mukhoza kukhala wa mpingo wa Khristu, koma inu simuli a Khristu

mpaka mzimu wanu utanena “ameni” ku lonjezo lirilonse limene Mulungu anapanga. Ndipo pamene Iye analonjeza. . .

¹⁷⁰ Petro anati, pa Tsiku la Pentekoste, iye anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mukhale mutabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Ndipo ngati mzimu wanu ukunena kuti izo zinali za tsiku lina. . . Kodi Lemba linati chiyani? “Pakuti lonjezo liri kwa inu,” Myuda, “ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo akutali,” Amitundu, “ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana.” Lonjezo lomwelo.

¹⁷¹ Iye anati, “Ine ndine Mpesa, inu ndinu nthambi.” Ndipo ngati icho chiri Chiphunzitso cha nthambi, nthambi yoyamba, nthambi yachiwiri iyenera kukhala ndi Chiphunzitso chomwecho. Ndipo Chiphunzitso chomwecho chidzabala zotsatira zomwezo. Ndipo pamene nthambi iliyonse ibwera pa Mpesa, iyo idzabala chinthu chomwecho. Ndine wokondwa, mmawa uno, ndine wokondwa kuti ine ndikudziwa kuti Mzimu wa Mulungu wamoyo ukuyankhulabe ndi kuyankhula kwa anthu, ndi kutsimikizira Mawu Ake.

¹⁷² Ife tikulowa mu utumiki wa ubatizo mu mphindi zochepa chabe. Ngati inu munakonkhedwa, kutsanuliridwa, kapena kumizidwa mwanjira iliyonse kuposa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, inu mukufunsidwa kuti mubwere ku madzi.

¹⁷³ Tsopano inu mukuti, “M’bale Branham, kodi inu mungatanthauze kuti mudiuze ine?” Inde, m’bale.

¹⁷⁴ Kukonkha sikunatchulidwe mu Baibulo. Palibe malo mu Baibulo pamene aliyense anayamba wakonkhedwapo. Tsopano kumbukirani izi. Ine ndafunsa desiki ili, sabata yonse. Ndipezereni ine pamene munthu mmodzi mu Baibulo anayamba wakonkhedwapo ku chikhululukiro cha machimo awo, anatsanuliridwapo ku chikhululukiro cha machimo awo, kapena kubatizidwa konse mwa kumizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” ku chikhululukiro cha machimo awo. Panalibe munthu anayamba wakonkhedwapo, kutsanuliridwa kapena kubatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera,” mu zikutiro zonse za Baibulo. Ayi, bwana. Iwo anali. . .

¹⁷⁵ Panali anthu ena anabatizidwa nthawi ina ndi Yohane M’batizi, ndipo iwo sanabatizidwe mu dzina lirilonse nkomwe, ndipo iwo anabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu. Koma Paulo, pamene iye anakomana nawo iwo mu Machitidwe 19, anawauza iwo kuti amayenera kubwera ndi kudzabatizidwanso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu, kapena iwo sakanakhoza kulandira Mzimu Woyera monga apobe.

176 Pamene Petro anawapeza ena amene analandira Mzimu Woyera asanabatizidwe nkomwe, iye anawalamulira iwo ndipo anakhala nawo iwo mpaka iwo anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Izo nzoona, mzanga.

177 Ine ndikudziwa anthu ambiri amati, “Tsopano, M’bale Branham ndi wa Yesu Yekha.” Ndizo zolakwika.

178 Ine ndimangokhulupirira Malemba. Ine sindine wa chipembedzo chirichonse. Ndipo a Yesu Yekha samabatiza mwanjira imeneyo, mulimonse. Iwo amangobatiza, Dzina la “Yesu.” Baibulo linati, “Ambuye Yesu Khristu.” Pali a Yesu ambiri, koma mmodzi yekha Ambuye Yesu Khristu. Mukuwona? Mukuwona? Khristu ndiye Mesiya. Mukuwona? Ndipo ndiko kulondola.

179 Ndipo tsopano, abwenzi, tsopano, inu amene muli pano mmawa uno, inu simunayambe mwabatizidwapo mwanjira imeneyo, mulole Liwu laling’ono lodekha la Mulungu liyankhule pansu mozama mmoyo wanu. Ndipo mosasamala za zomwe bishopu, zomwe mpingo, zomwe china chirichonse chikunena, bwerani ndi kudzamvera Ambuye, ndilo lamulo langa kwa inu.

180 Ndipo, tsopano, M’bale Neville apita ku chipinda *ichi*, kwa kukonzekera utumiki wa ubatizo. Ndi iwo omwe ali—akukonzekereza zinthuzo, ena mwa akulu ampingo apita ndi ine. Ine ndikhala ndi inu mmenemo, mu miniti yokha.

181 Koma ine ndikufuna iwo amene akubwera tsopano, pamene ife tidzayimba, “Ine ndikukhoza kumva Mpulumutsi wanga akuitana.” “Ine ndidzapita ndi Iye. Mosasamala zomwe mpingo, ine ndidzapita ndi Iye. Mosasamala zomwe aliyense, ine ndipita ndi Iye njira yonseyo.” Lolani a—amunawo apange njira yawo ku chipinda *ichi*, ndipo akazi apange njira yawo ku chipinda *ichi*, pamene ife tikuyimba tsopano. Ndiye ife tibalalitsidwa, movomerezeka, mu mphindi yokha tsopano. Chabwino. Tonse palimodzi tsopano.

Ine ndikumumva Mpulumutsi wanga akuitana,

182 Tsopano, amuna apite *kuno*, akazi cha *kuno*.

. . . Mpulumutsi wanga . . .

Akazi ena alowe *umu* ndi akazi awa chonde.

Ine ndikumumva Mpulumutsi wanga akuitana . . .

Inu mwamva chiyani? Liwu Lake.

“Tenga mtanda Wanga, ndi kunditsata, kunditsata Ine.”

Kumene Iye . . . (Tsopano kodi inu mukutanthauza kwenikweni?) . . . Ine ndidzamsatira,

Komwe Iye anditsogolera ine ndidzamsatira,

Komwe Iye anditsogolera ine ine
ndidzamsatira,
In ndinka Naye, Naye njira yonseyo.

¹⁸³ Tsopano, pamene ine ndikunena izi, mzanga, ine ndinamva Liwu. Ndipo ngati Liwulo silinayankhule molingana ndi Liwu la Mulungu, *Apa*, ndi liwu lolakwika. Koma, “Nkhosa Zanga zimadziwa Liwu Langa.”

¹⁸⁴ Kodi inu mungakhoze bwanji kubwera? Ichi ndi chifukwa chomwe inu mwabwerera. Ndi chifukwa, “Dzina lanu linayikidwa pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa asanaikidwe maziko a dziko lapansi.” Baibulo linanena chomwecho. Taganizirani za munthu amene wakhala pansi ndipo akudziwa kuti ndicho Choonadi cha Uthenga, ndipo komabe chinachake chikuwagwira iwo, podziwa kuti mwina dzina lawo silinaikidwepo. Ndiye chiyani?

“Pachabe iwo amandipembedza Ine.” Onani, “Pachabe.”

¹⁸⁵ “O,” inu mukuti, “Ndine munthu wokhulupirika. Ndine wokhulupirika . . .” Izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi izo.

¹⁸⁶ “Pachabe iwo amandipembedza Ine, kuphunzitsa ngati chiphunzitso malangizo a anthu.”

¹⁸⁷ Ine ndakuuzani inu, palibe aliyense anakonkhedwa, kutsanuliridwa, kapena kubatizidwa, mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” mu Baibulo. Fufuzani Izo. Pezani izo. Ngati izo ziri, bwerani mudzandisonyeze ine, pa nsanja usikuuno. Ndiye, ngati inu mwachitidwa mwanjira imeneyo, inu mukutsatira miyambo ya anthu.

¹⁸⁸ Ndipo ngati wina akuuzani inu, “Chabwino, inu mubwere ndi kudzapanga kuvomereza kwanu, inu mulandira Mzimu Woyera ndiye.” Ndizo zolakwika. Ndicho chiphunzitso chopangidwa ndi anthu.

¹⁸⁹ Pali ubatizo wamadzi wabodza. Pali ubatizo wa Mzimu Woyera wabodza. Mdierekezi amatsanzira Iwo chifukwa iye ndi wachipembedzo. Kaini, abambo ake anali achipembedzo, monga ife tadutsira mu izo. Mbewu ya serpenti ikupitirirabe. Ndipo Mbewu ya mkazi, kudzera mwa Khristu, ikupitirirabe.

“Koma, palibe munthu angakhoze kubwera kupatula Atate Anga atamukoka iye.”

¹⁹⁰ Tsopano taganizani za ena akhala pano, mmawa uno, amene mukudziwa kuti inu munabatizidwa mwabodza, mu kachikhulupiro ka munthu, ndipo osati molingana ndi Baibulo, ndipo kubadwa kwanu koyamba kwa kuvomereza ndi kolakwika. Iwe ungakhoze bwanji kukhala wolondola, kupatula ngati iwe ubwerera mmbuyo ndi kukayamba molondola? Inu mukukumbukira, sabata ino, ine ndalalikira: *Izo Sizinali Choncho Kuyambira Pachiyambi*.

¹⁹¹ Tsopano, ndipo ngati inu mungakhoze kumva Liwu likuyankhula kwa inu, ameneyo ndi Mulungu, chifukwa Ilo limagwirizana ndi Lemba. Ngati ilo silitero, ndiye kuti pali mtundu wina wa liwu lolakwika lomwe likuyankhula kwa inu. Koma Liwu lolondola lidzakuuzani inu kuti muzitsatira malamulo a Baibulo; palibe kukonkha, palibe kutsanulira, palibe mwabodza. Bwerani molunjika ndi kutsatira malamulo a Baibulo.

¹⁹² Chitani izo, abwenzi, ngati izo zinatengera chirichonse. Ine sindikusamala zomwe zingatengere, ine ndiyika pambali chirichonse, kuti ndimutsatire Ambuye Yesu.

¹⁹³ “Imvani Liwu Langa. Nkhosa Zanga zidzatero, ndipo zidzabwera kwa Ine. Ndipo onse amene ati adzadze kwa Ine, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo wosatha, ndi kumuukitsa iye mmasiku otsiriza.” Ndi kulondola iko?

¹⁹⁴ Ndi izi apa, limodzi ndi Malemba. Palibe amene angatsutse Izo. Uko nkulondola. Palibe amene angatsutse Izo. Ndi izi apa, mu Mphamvu ya Mzimu, kuchita zinthu zomwezo zimene Yesu anachita. Apa Iye ali, pa chithunzi, Lawi la Moto lomwelo, likusuntha, zipatso zomwezo, Mzimu womwewo, ukukhala nako kumverera komweko, kachitidwe komweko, zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo. Ndi inu apo. Imvani Liwu la Mulungu mmawa uno.

Ndipo Liwulo linati, “Samueli.”

¹⁹⁵ Anati, “Inde, Ambuye. Inde, Ambuye. Ndi ine pano. Pano pali wantchito Wanu. Pano pali wantchito Wanu. Ine nditsatira.”

Mulungu amudalitse donayo. “Ndidza . . .”

¹⁹⁶ Inu mukuti, “M’bale Branham, inu mumazipanga izo kukhala zolimba kwambiri.” Ine ndikutanthauza kwa izo kuti zikhale zolimba. Ziri pakati pa Moyo ndi imfa, kotero ine ndikuyenera kuzipanga izo zolimba. Ambuye akhale nanu, ndilo pemphero langa loonamtima.

¹⁹⁷ Tsopano, iwo asanasunthe mipando ya mnyumbayi kuno, kuti tikhale nawo. . . kuti inu mukhoze kuwona ubatizo. Malowa amakhala otsegula nthawi zonse. Ine ndikufuna kuti ndiwerenge zina, molunjika kumene kuchokera m’Malemba, kotero kuti inu muwone kuti ine ndiri—ine ndikuwerenga.

¹⁹⁸ Yesu Khristu, mu mutu wa 16 wa Mateyu Woyera, ine ndikukhulupirira, anamuwuzza Petro, “Ine ndikupatsa iwe mafungulo a ku Ufumu wa Kumwamba. Chirichonse chimene iwe umanga pa dziko lapansi, Ine ndidzachimanga Kumwamba; chirichonse chimene iwe uchimasula pa dziko lapansi, Ine ndidzachimasula Kumwamba.” Inu nonse mukudziwa zimenezo?

¹⁹⁹ Pa Tsiku la Pentekoste, pamene Ufumu wa Mulungu unadza mu chidzalo cha Mphamvu Yake, kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Petro, atayima. Tsopano, pamene Yesu anauka kwa

akufa, Iye analibe mafungulo a ku Ufumu. Ndi kulondola uko? [“Ameni.”] Iye anali nawo mafungulo a imfa ndi hade, osati mafungulo a ku Ufumu. Ndipo apa pali chimene iye ananena pamene iye anali kulalikirira, ndipo iwo anali kumva zinthu izi, ndipo anaumitsa mitima yawo. Izi ndi ndendende zomwe Petro ananena.

²⁰⁰ Tsopano mvetserani mwatcheru pamene ine ndikuwerenga Malemba, kotero kuti inu mukhoze kumvetsa. Machitidwe, mutu wa 2. Kumbukirani. Ndi angati anali pano kuti amve ulaliki, *Izo Sizinali Choncho Kuyambira Pachiyambi?* Tiyeni tibwerere ku chiyambi ndi kuwona chimene ubatizo, ubatizo uli kwenikweni. Kodi ife tiyenera kubatizidwa motani? Kukonkhedwa, kutsanuliridwa, kapena mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera”?

²⁰¹ Kumbukirani, ine ndatsutsa mtumiki aliyense, bishopu aliyense, aliyense, kulikonse, nthawi iliyonse, kuti andisonyeze ine Lemba limodzi pamene munthu aliyense anayamba wakonkhedwapo, kutsanuliridwa, kapena kubatizidwa mu dzina la “Atate, Mwana, Mzimu Woyera.” Ndi zapoyera. Izo siziri m’Malemba. Ayi.

²⁰² Ndizo zabodza, kachikhulupiriro kopangidwa, koyambitsidwa ndi mpingo wa Katolika. Kukonkha kunapangidwa ndi mpingo wa Katolika, pafupifupi zaka sikisi khandiredi pambuyo pa imfa ya wophunzira wotsiriza. A “Atate, Mwana, Mzimu Woyera” zinatengedwa nthawi yomweyo, chifukwa anthu a Chikatolika amapembedza milungu yosiyanasiyana, ndipo iwo anapanga utatu wa maudindo a Mulungu. Osati Amulungu atatu; Atate, Mwana, Mzimu Woyera. Ndizo zachikunja.

²⁰³ Pali Mulungu mmodzi. “Inu musakhale nayo milungu ina pamaso Panga.” “Imva iwe, O Israeli, Ndine Ambuye Mulungu wako, Mulungu mmodzi.”

²⁰⁴ Myuda anatifunsa ife kuti, “Ndani ali Mulungu wanu; Atate, Mwana, kapena Mzimu Woyera?”

²⁰⁵ Apo Mmodzi yekha wa iwo. Ndi maudindo atatu omwe Mulungu yemweyo wagwiramo ntchito, kudziwonetsera Yekha.

²⁰⁶ Poyamba, mwa Atate, sakanakhoza kukhudzidwa. Anapachikidwa pa phiri; ngakhale ng’ombe kapena chiweto chikakhudza phirilo, chimayenera kuphedwa.

²⁰⁷ Ndiye Iye anatsika pansu, chifukwa Iye ankafuna kuti adzipembedzedwa. Iye anayandikirira kwa munthu, chifukwa Iye anakhala Mwana wa munthu. Mulungu anali mwa Iye.

²⁰⁸ Ndipo pamene Iye anachita izo, ndiye Iye anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Komabe, inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine,” pronau ni yaumwini, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumapeto a

dziko.” Anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu.” Chiyani? Lawi la Moto. “Ine ndikubwerera kwa Mulungu.” Iye anatero? Iye anatero. Ndiyeno pamene Iye anachita izo, Iye anabwerera kwa Mulungu.

²⁰⁹ Ndiye ife tikumupeza Paulo, mu phunziro lathu mmawa uno, pa ulendo wake waku Damasiko. Ndipo Iye anamupeza Paulo ali panjira. Ndipo Iye anamukanthira iye pansi. Ndipo pamene Paulo anayang’ana mmwamba, Iye anali chiyani? Lawi la Moto kachiwiri, Kuwala kumene kunatulutsa maso ake.

²¹⁰ Penyani chimene Yesu anachita pamene Iye anali pa dziko lapansi, ndipo anamuza mkaziyo machimo ake, anachita zinthu zonse izi. Ndipo anati, “Ine sindimachita kanthu pokhapokha Atate atandiwonetsera Ine poyamba.”

²¹¹ Iwo anamufunsa Iye, anati, “Bwanji Inu osapita kumeneko ndi kukawachiritsa anthu awo kumeneko?” Anadutsa pakati pa khamu lalikulu la anthu, kumene olumala, otsimpfina, akhungu, ndi opuwala. Iye anamuchiritsa mwamuna wa vuto la prostate, kapena chinachake, atagona pa mphasa. Anati, “Bwanji Inu simukupanga gulu lonse la iwo?”

²¹² Iye anati, “Indetu, indetu. . .” Yohane Woyera 5:19, tsopano, “Indetu, indetu, Ine ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha; koma chimene Iye awona Atate akuchita, chimenecho achita Mwanayo.”

²¹³ Apa Iye wabweranso kachiwiri, mmasiku otsiriza ano. Dziko lasayansi silingakhoze kutsutsa izo. Mpingo sungakhoze kuzitsutsa izo. Ndi izi apa, kubwereranso mu mpingo ndi kumachita chinthu chomwecho. Mzimu! Mulungu akufuna amene adzapembedza mu Mzimu ndi mu Choonadi. Apa Iye ali.

²¹⁴ Izi ndi zomwe Iye ananena pa Tsiku la Pentekoste, Petro akulalikira.

Yesu ameneyu Mulungu wamuukitsa, ali kuti. . .ife tonse ndife mboni. (Kodi ndife mboni?)

Chifukwa chake pokhala pa dzanja lamanja la Mulungu anakwezedwa, . . . atalandira kwa Atate lonjezo la Mzimu Woyera, iye wakhetsera ichi, chimene inu muchiona ndi kumva tsopano.

Pakuti Davide sanakwere kulowa. . . kumwamba: koma iye ananena yekha, AMBUYE anati kwa Mbuye wanga, Khala pa dzanja langa lamanja,

Kufikira nditaika adani ako chopondapo mapazi ako.

Choncho nyumba yonse ya Israeli idziwe motsimikizika, kuti Mulungu anamupanga Yesu yemweyu, amene inu munampachika, zonse Ambuye ndi Khristu.

Tsopano pamene iwo anamva ichi, (awo anali anthu achipembedzo) pamene iwo anamva ichi, iwo analasidwa mu mtima mwawo, ndipo iwo anati kwa Petro ndi...atumwi ena otsalawo, Amuna ndi abale, kodi ife tidzachita chiyani?

215 Kodi ife tingopita ndi kukakhala abwino? Ayi, ayi. Samalira, Petro, iwe uli ndi mafungulo a ku Ufumu tsopano. “Chomwe iwe wawauza iwo,” Mulungu ananena, “Ine ndichitseka icho Kumwamba pamene iwe wachitseka icho padziko lapansi.”

Petro anati kwa iwo, Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndipo mukhale mutabatizidwa mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo omwe ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana.

216 Lemba linanso. Zaka sate thuu zitatha zimenezzo, Paulo, cha apa mu mutu wa 19.

Paulo atadutsa magombe akumtunda kwa...Efeso: iye anapeza ophunzira ena,

Ndipo iye anati kwa iwo, Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?

217 Abaptisti, mulole izo zilowerere mwa inu. “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?” Ndi kubadwa, osati kuvomereza.

...Ife sitikudziwa kumene kuli Mzimu Woyera uliwonse.

Ndipo iye anati...Kwa chiyani...inu munabatizidwira ndiye? Iwo anali atabatizidwa, Kwa Yohane...

Paulo anati kwa iwo, Yohane ndithudi ankabatiza... ku kulapa, (osati ku chikhululukiro cha machimo), ku kulapa, kunena...kuti inu mukhulupirire pa iye amene ali mkudzayo...ndiko kuti, pa Yesu Khristu.

Ndipo pamene iwo anamva izi, iwo anabatizidwa mu dzina la Ambuye Yesu Khristu.

...ndipo Paulo anayika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo; ndipo iwo anayankhula mu malirime, ndipo anamukweza Mulungu.

218 Tsopano ndiloleni ine ndikutengereni inu, Paulo, akutseka kalata yake, Agalatiya 1:8.

...ngakhale ife, kapena mngelo wochokera kumwamba, alalikirira kwa inu uthenga wina uliwonse


wosiyana ndi umene inu munaumva kale, muloleni iye akhale kwa inu temberero.

²¹⁹ Ine ndikhoza kukutengerani inunso ku Akorinto, mutu wa 14, ndime ya 38, pamene Ilo linanena.

Ngati munthu wina adzinenera kukhala wauzimu, kapena mneneri, muloleni iye azindikire kuti. . . zimene ine ndikukulemberani inu ali malamulo a Ambuye.

Koma ngati iye akhala mbuli, basi ingomusiyani iye akhale mbuli.

²²⁰ Kodi ife tichita chiyani za izo? Umboni uliwonse. . . Ine ndinali m'malo mwanu, ndipo sindinabatizidwe monga mwa ubatizo Wachikristu, mosasamala kanthu za zomwe mpingo wanga unkaganiza, kapena zomwe amayi anga ankaganiza, ine ndikufuna kuti ndidziwe zomwe Ambuye wanga akulamula.

²²¹ Ambuye Yesu, ndi Anu tsopano. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mugwire ntchito pa mtima uliwonse. Ndipo apatseni awa, amene ali mu dziwe kuti abatizidwe, Mzimu Woyera, pamene iwo akuyembekezera pa Inu. Mu Dzina la Yesu ife tikupereka unyinjiru kwa Inu, kuti pa Tsiku limenero, Ambuye, mulole ine ndisadzakhale wolakwa, koma womasuka ku mwazi wa anthu onse; osati kuyima ndi mwambo wina, kapena chipembedzo china, kapena bungwe, koma pa kuyima ndi Mawu Anu. Amenii. 

58-1005M Imvani Liwu Lake
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org